



Kalonga Wachete

Sheykh-e-Tarbiyat, Ameen-e-Ahli-Sunnat
Mujamhidul-e-Da'wat-e-Islami, Allamah Madaniya Abu Bilal

MUHAMMAD ILYAS

Attar Qadiri Razavi

Lawsonville, Maryland, USA and Karachi, Pakistan, in Dawat-e-Islami

خاموش شہزادہ

Khamosh Shahzanah

MWANA WANFUMU WAM'MUNA WACHETE

Uthengawu (Bayan) unaperekedwa ndi Shaykh-e-Tareeqat, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat, yemwe muyambitsi wa Dawat-e-Islami, 'Allamah Maulana Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi **دَامَتْ بَرَكَاتُهُمُ الْعَالِيَةِ** mu chilankhulo cha Urdu. Nthambu ya Majlis-e-Tarajim (thambi yomasulira) yamasulira uthengawu m'Chichewa. Ngati mungapeze cholakwika chilichonse pakumasulira kapena pakulemba kwake, chonde dziwitsani nthambi yomasulira kudzera pa keyala kapena imelo ili m'munsiyi, ndi cholinga chofuna kupeza mphotho [Sawab].

Translation Department (Dawat-e-Islami)

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

UAN: ☎ +92-21-111-25-26-92 – Ext. 7213

Email: ✉ translation@dawateislami.net

Mwana Wanfumu Wam'muna Wachete

Kumasulira m'chichewa kwa 'Khamosh Shahzanah'



MA UMWINI ONSE NDI OTETEZEKA

Ufulu © 2026 Maktaba-tul-Madinah

Palibe gawo lililonse la bukuli likuloledwa kusindikidzidwanso, kapena kusinthidwa, mukawonekedwe komanso munjira iliyonse ngati, ya magetsi, zipangizo zilizonse, kupanga kope kumene, kusungidwa kapena njira zina, popanda chilorezo cholembedwa ndi Maktaba-tul-Madinah.

Kutsindikidza kwa chiwiri: Ramaḍān-ul-Mubārak, 1447 AH – (Feb, 2026)

Lamasuliridwa ndi: Translation Department (Dawat-e-Islami)

Wosindikiza: Maktaba-tul-Madinah

Kuchuluka kwake: 5000

KUTHANDIZA

Khalani omasuka kulumikizana nafe ngati mukufuna kuthandizira kusindikiza kwa buku lachipembedzo kapena kabuku kuti likhale Isal-e-Sawab kwa achibale anu omwe anamwalira.

MAKTABA-TUL-MADINAH

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

✉ Email: maktabaglobal@dawateislami.net –
maktaba@dawateislami.net

☎ Phone: +92-21-34921389-93 – 34126999

🌐 Web: www.dawateislami.net

أَلْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى خَاتَمِ النَّبِيِّينَ
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

Du'a Powerenga Buku

Werengani Du'a (pempho) ili m'munsiyi musanayambe kuphunzira buku lachipembedzo kapena phunziro lililonse la Chisilamu, ndipo mudzakumbukira chilichonse chomwe mwaphunzira, *إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّ وَجَلَّ*:

اللَّهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَاَنْشُرْ
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْاِكْرَامِ

Kumasulira

O Allah *عَزَّ وَجَلَّ*. Titsegulireni khomo la chidziwitso ndi nzeru, ndipo tichitireni chifundo! Inuyo amene muli Olemekezeka komanso Wawulemelero koposa!

(Al-Mustatraf, vol. 1, tsamba. 40)

Dziwani: Nfunireni zabwino Mtumiki (Salat-‘Alan-Nabi ﷺ) kamodzi musanayambe komanso mukamaliza Du'ayi.

ZANKATIMU

MWANA WA NFUMU WA M'MUNA WA CHETE *	1
Ubwino wonfunira zabwino Mtumiki (Salat-'Alan-Nabi ﷺ)	1
Kukhala chete kumabweretsa chitetezo	3
Bahraam ndi mbalame	3
Mahadees anayi okhudza ubwino wakukhala chete	3
Kumasulira kwa 'kuposa zaka 60 zamapembedzo'	4
Zovuta zinayi zowopsa za kulankhula zosafunika	5
Chinthu chowononga kwambiri	7
Lankhulani zabwino kapena khalani chete	8
Ngati mukulakalaka paradizo ndiye, ...	8
Kukhala chete ndi njira yotetezera chikhulupiriro [Iman]	9
Kukhala chete ndichophimba kwa munthu osadziwa	10
Kukhala chete ndi makiyi a kulambira	10
Kuteteza kwa chuma ndi kophweka, koma uko kwa lilime. ...	10
Munthu amene amayankhula kwambiri pambuyo pake amanong'oneza bondo	11
Kuli bwino kunong'oneza bondo chifukwa chokhala chete nkusiyana ndi kunong'oneza bondo chifukwa choyankhula	12
Munthu wosalankhula ndi wotetezeka kwambiri	13
Kodi pakhomo pangakhale bwanji pa ntendere?	14
Njira ya Madani yothesera mikangano pakati pa mpongozi wankazi ndi apongozi ake	14
Chopempha kwa lilime	16
Ubwino woyankhula zabwino	17
Mtumiki ﷺ anakonda kukhala chete nthawi zonse	17

Mitundu iwiri ya mayankhulidwe ndi mitundu iwiri ya kukhala chete.....	18
Kumasulira kwa mayankhulidwe onyasa	19
Mafinya komanso magazi zizidzatuluka nkamwa.....	21
Munthu amene adzakhale ndi mawonekedwe a galu	22
Paradizo ndi Haraam [yoletsedwa]	22
nkanda wa Farooqi wa ngale zisanu ndi ziwiri za Madani.....	22
Ngati ndizokhazo zikuyenera kukhala choncho!	23
Chinsinsi cha m'nzake wa Mtumiki chokhala m'modzi mwa anthu aku paradizo	24
Zitsanzo za mayankhulidwe opanda phindu	25
N'kovuta kwa amene amayankhula zopanda phindu kudziletsa ku tchimo la kukuza nkhani (kunama)	28
Bwenzi titalandira n'dalitso lodikira komanso kuyeza zomwe tilankhule	29
Zokambirana zopanda phindu zokhudza uchigawenga.....	29
Siddeeq-e-Akbar ankayika mwala n'kamwa mwake.....	31
Kuphunzira kukhala chete kwa zaka 40.....	31
Woyera wa Taabi'i amene ankasinkhasinkha zokambirana zake polemba.....	32
Njira yodziwerengera pa zokambirana	33
Umar Bin 'Abdul 'Azeez analira kwambiri	34
Kufotokozero kwa nkhaniyi	35
Mankhwala apadera oyeretsera zokambirana kuchokera ku zopanda pake.....	36
Munthu wopusa amalankhula asanaganize	38
Njira yoyezera musanalankhule.....	39
Njira yosonyeza kukhala chete.....	40

Itanani mwawulemu ndipo pezani mphoto.....	42
ZODABWITSA ZITATU ZA MADANI ZOMWE	
ZINAWONEKERA CHIFUKWA CHA KUKHALA CHETE.....	44
1. Kuwona Mtumiki woyera chifukwa cha ubwino wa kukhala chete.....	44
2. Udindo wa kukhala chete pokhazikitsa chikhalidwe cha Madani	46
Chida cha Madani pa ntchito za Madani.....	47
3. Udindo wa kukhala chete pokhazikitsa chikhalidwe cha Madani m'nyumba	48
Ngale 19 za Madani zokhazikitsa chikhalidwe cha Madani m'nyumba	50
Madani 20 okhudza Miswak	56
KOCHOKERA MAWUMBONI	62

الْحَمْدُ لِلَّهِ رَبِّ الْعَالَمِينَ وَالصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ عَلَى خَاتَمِ النَّبِيِّينَ
أَمَّا بَعْدُ فَأَعُوذُ بِاللَّهِ مِنَ الشَّيْطَانِ الرَّجِيمِ بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ

MWANA WANFUMU WA M'MUNA WACHETE *

Ngakhale Satana ayesetse motani kukulepheretsani kuwerenga kabuku aka, werengeni konse. Ngati simunakhale osamala pa kagwiritsidwe ntchito ka lilime lanu, mudzagwa misonzi malingana ngati ntima wanu uli wamoyo chifukwa chowopa Allah, *إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ*.

Ubwino wonfunira zabwino Mtumiki (Salat-'Alan-Nabi ﷺ)

Mtumiki Wankulu komanso Woyera kwambiri صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, 'Kuchita Zikr (kumukumbukira) Allah عَزَّوَجَلَّ mochulukira komanso kunfunira zabwino Mtumiki Kumachotsa umphawi (kusawuka kwambiri).' (*Al-Qaul-ul-Badi', tsamba. 273*)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Uthengawu (Bayan) unaperekedwa ndi Ameer-e-Ahl-e-Sunnat الْعَالِيَةِ pa nsonkhano wa sabata (nsonkhano wolimbikitsa kutsatira Sunnah) wa Dawate-Islami (bungwe la dziko lonse, lopanda ndale, lofalitsa uthenga wa Quran ndi Sunnah) pa tsiku la 9 la mwezi wa Jumadal Aakhir, 1432 AH (12-5-2011). Uthengawu ukuperekedwa pano utakonzedwanso m'madera ena.

[Majlis Maktaba-tul-Madinah]

Mwadzidzidzi, mwana wa nfumu anasanduka wachete. Nfumu, nduna, ndinso onse a pa maso pachifumu ananabwa kwambiri ndi zomwe zinachitika kuti asiye kulankhula. Aliyense anayesetsa kupanga chilichonse, koma kalongayo inapitirizabe kukhala duu. Ngakhale panali kukhala chete kumeneku, moyo wa tsiku ndi tsiku wa kalongayo sunasinthe, amachitabe zomwe amachita masiku onse.

Tsiku lina, kalonga wacheteyu anapita limodzi ndi anzake kukasaka mbalame. Atanyamula uta ndi muvi wake, iye anayimirira pansu pa ntengo wandiweyani, akuyang'anayang'ana mbalame nkati mwa ntengowo. Mwadzidzidzi, kulira kwa mbalame kunanveka nkati mwa masamba am'ntengowo. Nthawi yomweyo, iye anaponya muvi kulozera kumene kunkachokera phokosolo, ndipo mbalameyo inagwa pansu ili yovulazidwa ndi muvi. Mbalameyo inayamba kupapatika mwawululu kwambiri.

Pomwepo, kalonga wacheteyu anadzidzimuka n'kulankhula kuti, "Mbalameyi ikanakhala chete, ikanakhala pabwino, koma itangoyankhula, yasanduka cholinga cha muvi; ndipo zachisoni, chifukwa cha kulankhula kwakeku, inenso ndayankhula!

Chup rehmay mayn saw sukh hayn tu yeh tajribah ker lay

Ay bhai! Zaban per tu laga Qufl-e-Madinah

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 66)

Kukhala chete kumabweretsa chitetezo

Okhulupirira anzanga! Nkhaniyi ikhoza kukhala yopeka, koma ndichowonadi chosatsutsika kuti munthu woyankhulayankhula amakakamiza ena kuti ayankhule, amawononga nthawi yake komanso ya ena, ndipo nthawi zina amanong'oneza bondo chifukwa cha zomwe wanena. Nthawi zambiri, iye amayenera kukumana ndi mavuto ambiri chifukwa cha mawu akewo. Ndichowonadi chenicheni kuti malingana ngati munthu akhala chete, amakhala otetezeka ku zovuta zambiri.

Bahraam ndi mbalame

Kwanenedwa kuti, 'Bahraam anali atakhala pansu pa ntengo, pomwe ananva kulira kwa mbalame. Anayiponya muvi n'kuyipha, ndipo anayamba kunena kuti, 'Kusamala lilime kuli ndi phindu kwa anthu komanso mbalame. Mbalameyi ikanakhala kuti inasamala lilime lake, sikanaphedwa.' (*Al-Mustatraj, vol. 1, tsamba. 147*)

Mahadees anayi okhudza ubwino wakukhala chete

1. ﴿مَنْ صَمَتَ نَجًا﴾ kumasulira: amene wakhala chete wapulumuka. (*Sunan-ut-Tirmizi, vol. 4, tsamba. 225, Hadees 2509*)
2. ﴿الصَّمْتُ سَيِّدُ الْأَخْلَاقِ﴾ kukhala chete ndiko nfumu

yamakhalidwe onse. (*Al-Firdaus bima Saur-ul-Khattab, vol. 2, tsamba. 417, Hadees 3850*)

3. ﴿الصَّوْمُ أَرْفَعُ الْعِبَادَةَ﴾ kukhala chete kumakweza kupembedza. (*Ibid, Hadees 3849*)
4. Munthu akakhalitsitsa pakukhala chete ndizabwino kuposa zaka 60 zakupembedza. (*Shu'ab-ul-Iman, vol. 4, tsamba. 245, Hadees 4953*)

Kutanthawudza kwa Mawu akuti 'kuposa zaka 60 zakupembedza'

Wothirira ndemanga wotchuka wa Quran Yoyera, Hakeem-ul-Ummat, Mufti Ahmad Yar Khan عَلَيْهِ رَحْمَةُ الرَّحْمَان walemba motere pokhudza Hadees yachinayi: Ngati wina achita mapembedzo a zaka makumi asanu ndi limodzi (60), koma amayankhulanso kwambiri, ndipo sasiyanitsa pakati pa mayankhulidwe abwino ndi oyipa, ndiye kuti ndi bwino kukhala chete kwa kanthawi. Chifukwa n'kukhala chete, muli kusinkhasinkha, muli kudzikonza kwa Nafs (ntima/zilakolako zankati), muli kumira n'chowonadi cha umulungu ndi chizindikiritso, muli kulowa pansu pa nyanja ya Zikr yankati (kumukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ), komanso muli Muraqabah (kusinkhasinkha mozama). (*Mirat-ul-Manajih, vol. 6, tsamba. 361*)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Zovuta zinayi zowopsa za kulankhula zosafunika

Iwo amene amangocheza n'kumayankhulayankhula, amene amakonda kukangana pa zokambirana, komanso amene amayankhula zopanda phindu n'kumaganiza kuti n'kololedwa ndipo si tchimo, kapena iwo amene amayankhula zinthu zosafunika nthawi zonse, iwonso ayenera kuganizira maganizo a Hujjat-ul-Islam, Sayyiduna Imam Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْوَالِي pa nkhani ya mayankhulidwe opanda phindu. Ayenera kudzichititsa mantha okha ndi zovuta zinayi za kulankhula zopanda phinduzi. Ndi pa zifukwa zinayi izi pamene iye wadzudzula mayankhulidwe opanda phindu:

1. Kiraman Katibeen (angelo olemkezeka amene amalemba ntchito ndi zochita za anthu) ayenera kulemba zokambirana zopanda phindu, choncho munthu ayenera kuchita manyazi ndi zimenezi ndipo sayenera kuwavutitsa powapatsa ntchito yolemba zokambirana zopanda phindu. Allah عَزَّوَجَلَّ. akunena mu Vesi 18 ya Surah Qaaf mu gawo la 26:

مَا يَلْفِظُ مِنْ قَوْلٍ إِلَّا لَدَيْهِ رَقِيبٌ عَتِيدٌ ﴿١٨﴾

Samayankhula liwu limodzi munthu popanda mngelo wokonzeka kuti alembe.

[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Quran)] (Gawo 26, Qaaf, vesi 18)

2. Sidzabwino kuti buku la zochita lodzadza ndi zokambirana zopanda phindu liperekedwe n'khoti la Allah عَزَّوَجَلَّ.
3. Munthu adzalamulidwa pa maso pa a Allah عَزَّوَجَلَّ kwa zolengedwa zonse kuti awerenge buku lake la zochita. Panthawiyo, zowopsa zochititsa mantha za Tsiku la Chiweruzo zidzakhala pamaso pake; adzakhala wopanda zovala, kukhosi kwake kudzakhala kowuma ndiludzu kwambiri, nsana wake udzawerama chifukwa cha njala, adzakhala walepheretsedwa kulowa ku Jannah, ndipo ntendere wantundu uliwonse udzakhala watayika kwa iye.

Ganizirani bwino kwa mphindi imodzi! Zikanakhala zochititsa mantha bwanji kuwerenga buku la zochita lodzaza ndi zokambirana zopanda phindu panthawi yowopsa ngati imeneyi. (Ngati tiwerengera kuti munthu amalankhula zopanda phindu kwa mphindi 15 patsiku, zimapereka mawola 7.5 pamwezi, zomwe zimafika mawola 90 pachaka. Tiyerekeze kuti munthu amalankhula zopanda phindu pafupifupi mphindi 15 patsiku kwa zaka 50, izi zimapereka masiku 187 ndi mawola 12, ndiye kuposa miyezi 6. Choncho, ganizirani! Pa Tsiku lochititsa mantha la Chiwerudzo pamene dzuwa lidzakhala likuwotcha ngati moto kuchokera pa ntunda wa mayilosu amodzi, ndani angathe kuwerenga buku lake la zochita kwa miyezi 6 mosalekeza, popanda kupuma, m'kutentha kowopsa kotereku! Ichi ndi chiwerengero cha mphindi 15 zokha za zokambirana zopanda phindu patsiku; nthawi zina

timathera mawola ambiri tikungocheza zopanda phindu ndi anzathu, ndipo zokambirana za machimo ndi zoyipa zina zimawonjezera pa zimenezi).

4. Pa Tsiku la Chiwerudzo, zokambirana zopanda phindu za munthu zidzatsutsidwa, ndipo chifukwa cha zimenezi adzachita manyazi. Munthuyo sadzakhala ndi yankho, ndipo chifukwa cha manyazi pamaso pa Allah عَزَّوَجَلَّ adzanyozeka ndipo adzatuluka thukuta kwambiri. (*Minhaj-ul- 'Aabideen, tsamba. 67*)

Her lafz ka kis tarah hisab ah! Mayn doon ga

Allah zaban ka ho 'ata Qufi-e-Madinah

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 66)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Chinthu chowononga kwambiri

Sayyiduna Sufyan Bin 'Abdullah رَضِيَ اللهُ عَنْهُ ananena kuti: "Nthawi ina ndinapempha pamaso pa Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ kuti, 'Ya Rasoolallah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ! Ndi chinthu chiti chimene mungachizindikire ngati chowopsa kwambiri ndi chowononga kwambiri kwa ine?' Mtumiki Wokondedwa ndi Wodalitsika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ kenako anagwira lilime lake lodalitsika nati, 'Ichi.' (*Sunan-ut-Tirmizi, vol. 4, tsamba. 184, Hadees 2418*)

Lankhulani zabwino kapena khalani chete

Zikanakhala kuti! Hadeesi iyi ya Sahih Bukhari ikanakhazikika m'maganizo mwathu, yomwe imanena kuti:

مَنْ كَانَ يُؤْمِنُ بِاللَّهِ وَالْيَوْمِ الْآخِرِ فَلْيُكَلِّمْ خَيْرًا أَوْ لِيَصْمُتْ

“Amene wakhulupirira Allah ﷺ komanso Tsiku la Chiwerudzo, ayenera kulankhula zabwino kapena akhale chete.” (*Sahih Bukhari, vol. 4, tsamba. 105, Hadees 6018*)

Pa tsamba 91 la buku la ‘Allah-Walon ki Batayn’, lomwe lili ndi masamba 217, lofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yomasulira ya Dawat-e-Islami, Ameer-ul-Mu`mineen, Sayyiduna Siddeeq-e-Akbar رَضِيَ اللهُ عَنْهُ ananena kuti: ‘Palibe ubwino uliwonse m'mayankhulidwe amene sanapangidwe chifukwa chofuna kusangalatsa Allah ﷺ.’

(*Hilya-tul-Awliya, vol. 1, tsamba. 71*)

Sayyiduna Imam Sufyan Sawri رَضِيَ اللهُ عَنْهُ wanena kuti, ‘Gawo loyamba la mapembedzo, ndiko kukhala chete, lachiwiri ndiko kupeza chidziwitso, kenako ndiko kuchisunga m'mutu (kukumbukira), kutsatira poyenera kuchichita, ndipo potsiriza ndiko kuchifalitsa kwa ena’. (*Tareekh-ul-Baghdad, vol. 6, tsamba. 6*)

Ngati mukulakalaka paradizo ndiye, ...

Anthu anapempha pa maso pa Sayyiduna ‘Isa عَلَيْهِ الصَّلَاةُ وَالسَّلَامُ,

'Tiwuzeni chinthu chomwe tingachite kuti tikalowe ku paradizo.' Iye عَلَيْهِ السَّلَامُ anayankha, 'Musamayankhule nkomwe.' Kenako iwo anati, 'Sizingatheke kupeweka,' pomwe iye anati, 'musatulutse chilichose palirime lanu kupatula chomwe chili chabwino.'

(Ihya-ul-'Uloom, vol. 3, tsamba. 136)

Akser mayray hontaun pay rahay Zikr-e-Madinah

Allah zaban ka ho 'ata Qufl-e-Madinah

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 66)

Kukhala chete ndi njira yotetezera chikhulupiriro

[Iman]

Munthu amene nthawi zonse amadula mawu aanthu ena ngati Lumo, adzakhala opanda chidziwitso cha zomwe winayo akunena. Ndipo kwenikweni, pamakhala ngozi yayikulu kwa munthu woyankhulayankhula kuti pamene akupitiriza kulankhula, مَعَاذَ اللَّهِ عَزَّوَجَلَّ mawu achipongwe, (Kufriyat) akhodza kumpulumuka m'lilime lake.

Pofotokoza mawu a ena mwa akuluakulu opembedza, (awliya) Hujjat-ul-Islam, Sayyiduna Imam Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْوَالِي wanena m'buku la Ihya-ul-'Uloom, 'makhalidwe awiri amapezeka mwa anthu amene amakhala chete:

1. Chipembedzo chimakhala chotetezedwa, ndipo

2. Amanvetsa bwino zomwe winayo akunena.'

(Ihya-ul-'Uloom, tsamba. 137, vol. 3)

Kukhala chete ndichophimba kwa munthu osadziwa

Sayyiduna Sufyan Bin 'Uyaynah رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ wanena kuti, 'kukhala chete ndi ulemu wa munthu wophunzira (Alim) komanso ndichophimba cha wosadziwa.'

(Shu'ab-ul-Iman, vol. 7, tsamba. 86, Hadees 4701)

صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ صَلَّى اللَّهُ عَلَى الْحَبِيبِ

Kukhala chete ndi makiyi a kulambira

Zafotokozedwa kuchokera kwa Sayyiduna Imam Sufyan رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ, 'kukhala chete kwa nthawi yayitali ndiko makiyi a kulambira.'

(As-Samt ma' Mawsu'ah Ibn Abid Dunya, vol. 7, tsamba. 255, Hadees 436)

Kuteteza kwa chuma ndi kophweka, koma uko kwa lilime...

Sayyiduna Muhammad Bin Waasi' عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ التَّائِعِ ananena kwa Sayyiduna Maalik Bin Dinar عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْعَقَّارِ, 'kuteteza kwa lilime ndi chinthu chovuta kwambiri kwa munthu kusiyana ndi kuteteza chuma.' *(Ithaf-us-Sanah liz-Zabeedi, vol. 9, tsamba. 144)*

N'zonvetsa chisoni kuti aliyense amasamala kwambiri zotetedza chuma chake, ngakhale kuti chuma chikatha, ndi chitayiko cha dziko lino chabe. Koma m'mbuyo mwa izi, kudziretsa pa malankhulidwe n'kosowa kwambiri! Mosakayika, chifukwa chosatetedza lilime, pambali pa kutaya zinthu za n'dziko lino, palinso chiwopsezo chachikulu cha masawutso ku moyo uli nkudza.

Bak bak ki yeh 'aanat na sar-e-Hashr phansa day

Allah zaban ka ho 'ata Qufl-e-Madinah

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 66)

Munthu amene amayankhula kwambiri pambuyo pake amanong'oneza bondo

Okonedwa abale anga a Chisilamu! Ndi chinthu chosatsutsika kuti munthu akakhala chete, mwayi wochititsidwa manyazi umakhala ochepa kwambiri. Koma munthu amene ali ndi chizolowezi cholankhula paliponse, nthawi zambiri amakakamizika kupepesa kapena amanong'oneza bondo mu ntima mwake kuti: 'Nkanakhala kuti sindinalankhule pa nthawiyo, zikanakhala bwino kwambiri.' Chifukwa choti ndinalankhula, ulemu wa munthu wina uja unatha, ndinanva mawu owawa, uyu anakwiya, uyo anakhumudwa, kapena ndinapweteka ntima wa wina, ndipo ulemu wanga unachepa, ndi zina zotero.

Zafotokozedwa kuchokera kwa Muhammad Bin Nadr Haarisi عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْقَوِي, 'Ulemu zimatha chifukwa choyankhula kwambiri.'

(As-Samt ma' Mawsu'ah Ibn Abid Dunya, vol. 7, tsamba. 60, Hadees 52)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Kuli bwino kunong'oneza bondo chifukwa chokhala chete nkusiyana ndi kunong'oneza bondo chifukwa choyankhula

Kwenikweni, kuli bwino kunong'oneza bondo chifukwa chokhala chete kusiyana n'kunong'oneza bondo pambuyo polankhula; ndiponso kuli bwino kunong'oneza bondo chifukwa chodya pang'ono kusiyana n'kunong'oneza bondo pambuyo podya mopitirira muyezo. Pakuti amene amalankhula kwambiri amakumana ndi masoka, ndipo amene ali ndi chizolowezi chodya kwambiri amasokoneza m'mimba mwake, nthawi zambiri amakhala wonenepa kwambiri (onona mwa matenda), ndipo amadwala nthenda zamitundu-mitundu.

Ngati, mwa mwayi, angapulume ku matenda pa unyamata wake, ndiye kuti unyamatawo ukatha, nthawi zambiri thupi lake limakhala likulu la matenda. Kuti muphunzire za kuwopsa kodya kwambiri, njira zochiritsira wonenepa kwambiri, ndi

zina zambiri, werengani mutu wa 'Ubwino wa njala'm' buku la Faizan-e-sunnat.

Munthu wosalankhula ndi wotetezeka kwambiri

Okondedwa abale achisilamu! Ngati titalingalira bwino, munthu wakhungu ali otetezeka kwambiri chifukwa amakhala otetezedwa ku machimo owona zinthu zoletsedwa, monga kuyang'anitsitsa akazi omwe si achibale (Na-Mahram), kuyang'ana anyamata mwachilakolako, kuwonera mafilimu ndi masewero a zisudzo, komanso kuyang'ana mawondo ndi ntchafu za munthu amene wavala kabudula wanfupi. Momwemonso, munthu wosayankhula amakhalanso otetezeka ku machimo osawerengeka a lilime.

Ameer-ul-Mu`mineen, Sayyiduna Abu Bakr Siddeeq رَضِيَ اللهُ عَنْهُ wanena kuti, 'Bwenzi nditakhala wosalankhula, koma ndinapatsidwa mwayi wongotha kutchula dzina la Allah عَزَّوَجَلَّ [Zikr] lokha.' (*Mirqat-ul-Mafatih, vol. 10, tsamba. 87, Hadees 5826*)

Zatchulidwa mu Ihya-ul-'Uloom kuti Sayyiduna Abu Darda رَضِيَ اللهُ عَنْهُ anawona nkazi wolankhulitsa kwambiri, ndipo anati, 'Akanakhala wosayankhula, Bwenzi zili bwino kwa iye.'

(*Ihya-ul-'Uloom, vol. 3, tsamba. 142*)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Kodi pakhomo pangakhale bwanji pa ntendere?

Kuchokera pa mawu a bwenzi la Mtumiki (Sahaba)

Wathu صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wokondedwa ndi wodalitsika رَضِيَ اللهُ عَنْهُ makamaka alongo athu achisilamu ayenera kutengapo phunziro, iwo amene amakhala otanganidwa ndi macheza opanda phindu ndipo satopa polankhula za izi ndi izo. Ngati alongo achisilamu atagwiritsa ntchito "Qufl-e-Madinah" (kutseka lilime) m'njira yoyenera, mavuto ambiri monga kusagwirizana m'nyumba, mikangano pakati pa achibale, komanso mikangano pakati pa mpongozi ndi mpongozi wake wankazi akhoza kutha. Ndipo pakhomoponse pangakhale malo a ntendere, chifukwa mikangano yambiri ya m'nyumba imayamba chifukwa cha kusagwiritsa bwino ntchito kwa lilime.

Njira ya Madani yothesera mikangano pakati pa mpongozi wankazi ndi apongozi ake

Ngati apongozi amayi an'kalipira kapena kumudzudzula mpongozi wawo, mpongozi wankaziyo ayenera kukhala oleza ntima komanso opirira kwambiri. Asayankhe ngakhale liwu limodzi kwa apongozi akewo, ndipo asanandawule kwa mwamuna wake. Asawuzire aliyense kwa makolo ake, ndipo asonyeze nkhope yosangalala osati yokwiya. Komanso asatulutsire nkwiyo wake pa ana kapena pa ziwiya za m'nyumba (monga mbale). Ngati atachita zimenezi,

kupambana kudzakhala naye. Akuti, 'Kukhala chete kamodzi kumathetsa mikangano zana imodzi.'

Momwemonso, ngati mpongozi wankazi ayamba kukangana ndi apongozi ake, apongoziwo asabwezere kalikonse. Iwo ayenera kukhala chete ndipo asadandawule kwa aliyense wa m'nyumba mwawo, ngakhale kwa mwana wawo wamwamuna

إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ Malinga ndi mwambi wakuti, 'Kukhala chete ndi golide' iye adzapeza ntendere komanso chisangalalo. Ngati mankhwala a Madani ochokera kwa Sag-e-Madinah (mlembi) awa atsapidwa moyenera, ndiye kuti mikangano yonse pakati pa mpongozi ndi apongozi idzathetsedwa posachedwa, ndipo pakhomu padzakhala malo a ntendere. Kutu mupeze mankhwala a mikangano ya pakati pa mpongozi ndi apongozi, pezani VCD yodzadza ndi ngale za Madani za nzeru, yotchedwa 'Ghar Aman ka Gehwarah Kaysay Banay' kuchokera ku Maktaba-tul-Madinah, kapena iwonereni pa webusayiti ya Dawat-e-Islami, www.dawateislami.net. Ndi madalitso a VCD imeneyi, mabanja ambiri omwe anali pa chisokonezo akhala malo a ntendere.

Hay dabdabah khamoshi mayn haybat bhi hay pinhan

Ay bhai! Zaban per tu laga Qufl-e-Madinah

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 66)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Chopempha kwa lilime

Okondedwa abale anga achisilamu! Lilime likakhala lowongoka, ndipo likamagwiritsidwa ntchito polankhula zabwino zokha, ndiye kuti thupi lonse lidzapindula ndi zimenezi. Koma ngati lili lokhotakhota—mwachitsanzo, limakalipira wina, kutukwana ndi kunyozetsa wina, kuchita miseche ndi kuneneza, komanso kunama—ndiye kuti nthawi zina ngakhale m'dziko lino thupi limalangidwa.

Mtumiki wa chifundo nkhalapakati wa Ummah, mwini Jannah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wanena kuti, 'Mtumiki wa Rahmah, nkhalapakati wa Ummah, mwini wa Jannah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, 'Munthu akadzuka m'mawa, ziwalozonse za thupi lake zimaweramira lilime ndikunena kuti, 'Opani Allah عَزَّوَجَلَّ chifukwa cha ife, chifukwa ife tili ogwirizana ndi inu. Ngati inu mukhala owongoka, ifenso tikhala owongoka; koma ngati inu muli opindika (okhotakhota), ifenso tikhala opindika.'

(Sunan-ut-Tirmizi, vol. 4, tsamba. 183, Hadees 2415)

Ya Rab na zarurat kay siwa kuch kabhi boloon!

Allah zaban ka ho 'ata Qufl-e-Madinah

(Wasail-e-Bakhshish, p. 66)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Ubwino woyankhula zabwino

Mtumiki wokonedwa ndi wodala صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, 'Ku Jannah kuli zipinda zam'mwamba zomwe kunjira kwake kumatha kuwoneka uli nkati, ndipo nkati mwake kumatha kuwoneka uli kunjira.' M'beduini (mloya wakumudzi) wina anayimirira ndikufunsa kuti, 'Ya Rasoolallah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ! Kodi zipindazi ndi za ndani?' Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anayankha kuti, 'Izi ndi za munthu amene amalankhula zabwino, amadyetsa ena, amasala kudya (motsatizana), komanso amadzuka usiku kupemphera Salah chifukwa cha Allah عَزَّوَجَلَّ pamene anthu ena ali ntulo.

(Sunan-ut-Tirmizi, vol. 4, tsamba. 237, Hadees 2535)

Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anakonda kukhala chete nthawi zonse

كَانَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ طَوِيلَ الصَّمْتِ

kumasulira: Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anakonda kukhala chete nthawi yayitali. *(Sharh-us-Sunnah lil-Baghwi, vol. 7, tsamba. 45, Hadees 3589)*

Wothirira ndemanga wotchuka, Hakeem-ul-Ummat, Mufti Ahmad Yar Khan عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللهِ الْكَفَّان analemba pomasulira Hadees imeneyi kuti, 'Kukhala chete kwatchulidwa pano kukutanthawuza kukhala chete ku nkhani za dziko lino, apo ayi lilime lodala la Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ nthawi

zonse linali lotanganidwa ndi Zikr za Allah **عَزَّوَجَلَّ**; iye sankalankhula ndi anthu popanda chifukwa chonveka.

Zimenezi zikutanthawuza zokambirana zololedwa; koma zokambirana zoletsedwa (zamachimo) sizinatuluke m'lilime lake lodala m'moyo wake wonse. Bodza, miseche, kuneneza ndi zina zotero, sizinatuluke m'lilime lodala ngakhale kamodzi m'moyo wake wonse wodala. Mtumiki Wolemekezeka **صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ** ndi chitsanzo cha chowonadi, choncho kodi bodza lingayandikire bwanji kwa iye!'

(Mirat-ul-Manajih, vol. 8, tsamba. 81)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Mitundu iwiri ya mayankhulidwe ndi mitundu iwiri ya kukhala chete

Mtumiki wathu wokondedwa ndi wodala **صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ** wanena kuti:

إِمْلَاءُ الْخَيْرِ خَيْرٌ مِّنَ السُّكُوتِ وَالسُّكُوتُ خَيْرٌ مِّنَ إِمْلَاءِ الشَّرِّ

Kulankhula zabwino ndi chinthu chopambana kusiyana ndi kukhala chete, ndipo kukhala chete ndikwabwino kuposa kulankhula zoyipa..

(Shu'ab-ul-Iman, vol. 4, tsamba. 256, Hadees 4993)

Sayyiduna 'Ali Bin 'Usman Hajwayri, wodziwika ngati 'Daata Ganj Bakhsh رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ' analemba m'buku lake Kashf-ul-Mahjoob: Kulankhula kuli m'mitundu iwiri, 'Koyamba ndikulankhula kwa chowonadi ndipo kwina ndikulankhula zabodza, chimodzimodzinso, kukhala chete kuli m'mitundu iwiri:

1. Kukhala chete kwa cholinga: (Mwachitsanzo, kukhala chete n'cholinga chofuna kusinkhasinkha za m'moyo wa pambuyo pa infa kapena malamulo a Chisilamu, ndi zina zotero), ndipo
2. Kukhala chete kopanda cholinga: (Kukhala chete komwe kuli kodzadza ndi maganizo oyipa kapena zofuna za dziko lino).

Sayyiduna Daata Ganj Bakhsh رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anafotokoza fanizo lowonetsa ubwino ndi kuyipa kwa makambirano:

Nthawi ina, Sayyiduna Abu Bakr Shibli Baghdadi رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ amadutsa m'dera lina ku Baghdad ndipo ananva munthu wina akunena kuti: أَلْسْكُوتُ خَيْرٌ مِنَ الْكَلَامِ (Kukhala chete kuli bwino kuposa kulankhula).

Iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anati, "Kukhala chete kwako n'kwabwino kwa iwe kuposa kulankhula, koma kwa ine, kulankhula kuli bwino kuposa kukhala chete.' (Kashf-ul-Mahjoob, tsamba. 402)

Kumasulira kwa mayankhulidwe onyasa

Ndi mwayi wawukulu bwanji kwa abale ndi alongo achisilamu

amene amagwiritsa ntchito malilime awo m'makambirano abwino komanso amene amapereka chi itano cha zabwino kwa anthu. Tsoka ilo, matsiku ano ndikosowa kwambiri kupeza misonkhano yopanda kulankhula zonyasa, mpaka kufika pamene iwo omwe amawoneka ngati opembedza satha kudziretsa pa zimenezi. Mwina sadziwa n'komwe kuti kulankhula zonyasa n'chani. Nvetserani! Kumasulira kwa kulankhula zonyasa ndi: **التَّعَبِيرُ عَنِ الْأُمُورِ الْمُسْتَقْبَحَةِ بِالْعِبَارَاتِ الصَّرِيحَةِ** 'Kutchula nkhani zachiwerewere (monga zonyatsa ndi zinthu zoyipa) m'mawu onveka bwino.' (*Ihya-ul-'Uloom, vol. 3, tsamba. 151*)

Achinyamata amene amayambitsa zokambirana za nkhani zachinsinsi za m'banja ndi zinthu zimene zimayenera kukhala zophimbidwa, n'cholinga choti akwaniritse zilakolako zawo, iwo amene amasangalatsa mitima yawo mwa kulankhula, kapena kunvetsera chabe nkhani zolawula ndi zachiwerewere, iwo amene amagwiritsa ntchito mawu otukwana onyansa, iwo amene amapanga zizindikiro zonyansa, iwo amene amapeza chisangalalo m'dzidzindikiro zolawulazi, ndi iwo amene amawonera mafilimu ndi masewero a zisudzo n'cholinga choti akwaniritse zilakolako zawo zonyansa (chifukwa nthawi zambiri m'zinthu zimenezi mumakhala chiwerewere chochulukwa) ayenera kuwerenga mobwerezabwereza nkhani yozetsa nkhowa yotsatirayi ndipo ayenera kunjenjemera ndi mantha a Allah Wamphanvu zonse **عَزَّوَجَلَّ**.

Mafinya komanso magazi zizidzatuluka nkamwa

Zasimbidwa kuti mitundu inayi ya anthu a ku Jahannama idzakhala ikuthamanga ndi kusokonezeka pakati pa madzi otentha ndi moto ndipo idzakhala ikupempha kuti iwonongeke. Ntundu umodzi mwa mitundu inayiyi idzakhala munthu amene n'kamwa mwake mudzakhala mukutuluka mafinya omanso magazi ndipo anthu aku Jahannama adzati kwa iye, 'Chachitika ndi chani ndi munthu watsoka uyu kuti amuwonjezera zowawa komanso mazunzo athu?' Yankho lidzaperekedwa kuti, 'Munthu watsoka ndi wovutika uyu anakonda kunvetsera makambirano onyansa ndipo ankapeza chisangalalo mwa kukambiralanako, monga nkhani zakugonana.' (*ithaf-us-sanah liz-zabeedi, vol. 9, tsamba.187*)

Iwo amene amapereka chidwi chawo kukunonong'oneza n'khutu a satana okhudza akazi a Na-Mahram ndi Amrads, iwo amene amadzilowetsa dala m'maganizo oyipa, ndipo مَعَادَ اللَّهِ onse amene amapeza chisangalalo mwa kulingalira zinthu zonyansa ayenera kutengapo chenjezo pa nkhani imene yatchulidwa pamwambayi.

Na waswasay aayain na mujhay ganday khiyalat

Day zihn ka or dil ka Khuda! Qufl-e-Madinah

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 66)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Munthu amene adzakhale ndi mawonekedwe a galu

Sayyiduna Ibraheem Bin Maysarah رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ wanena kuti, 'Munthu amene amalankhula zolawula (kutanthawuza, amene amalankhula zinthu zolawula) adzafika pa Tsiku la Chiweruzo ali ndi mawonekedwe a galu.' (*Ithaf-us-Sanah liz-Zabeedi, vol. 9, tsamba. 190*)

Paradizo ndi Haraam [yoletsedwa]

Mneneri wa Rahmah, nkhalapakati wa Ummah, Mwini Jannah صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ wanena kuti, 'Paradizo ndi Haraam kwa munthu amene amagwiritsa ntchito mawu olawula (kutanthawuza, amene amalankhula zinthu zolawula).' (*As-Samt ma' Mawsu'ah Ibn Abid Dunya, vol. 7, tsamba. 204, Hadees 325*)

nkanda wa Farooqi wa ngale zisanu ndi ziwiri za Madani

Ameer-ul-Mu`mineen, Sayyiduna 'Umar Farooq-e-A'zam رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ wanena kuti:

1. Iye amene amapewa kulankhula zopanda phindu amadalitsidwa ndi nzeru komanso luntha.
2. Iye amene amapewa kuyang'ana zopanda phindu mwachitsanzo, kuyang'anayang'ana m'mbali mosafunikira, amapeza bata la mu ntima.

3. Iye amene amadziletsa pakudya zopanda phindu (kutanthawuza, amene amadziletsa kudya mopitirira muyezo kapena kudya zakudya zamitundu yosiyanasiyana popanda njala koma chifukwa cha chisangalalo chabe) amapatsidwa chisangalalo mu 'Ibaadah (kupembedza).
4. Iye amene amadziletsa kuseka kopanda phindu amapatsidwa ulemu ndi kudzisunga.
5. Iye amene amadziletsa pakuchita nthabwala ndi chipongwe, amadalitsidwa ndi kuwala kwa Iman (chikhulupiriro).
6. Iye amene amadziletsa pakukonda dziko lino, amapatsidwa chikondi cha moyo wa pambuyo pa infa.
7. Iye amene amadziletsa pakupeza zolakwa mwa ena, amadalitsidwa ndi luso lokonza zolakwa zake.

(zatengedwa kuchokera mu: Al- Munabbihati, tsamba.89)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Ngati ndizokhazo zikuyenera kukhala choncho!

M'bale ndi mlongo aliyense wa Chisilamu ayenera kupanga kukhala chizolowezi chake kuwerenga kapepala aka pa Lolemba loyamba la mwezi uliwonse wa Madani (Chisilamu).

إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ Mudzanva kusintha kodabwitsa mu ntima mwanu.

Njira yabwino kwambiri yotetezera malilime athu ndiyo kuchita mogwirizana ndi Madani In'amaat nambala 45 ndi 46, chifukwa chake kuti mukhale ndi chizolowezi chopewa kulankhula zopanda phindu, malizitsani makambirano ofunikira m'mawu ochepa omwe angatheke, ndipo kuwonjezera apo yesetsani kulankhulana kudzera m'nzizindikiro komanso kudzera m'nzolemba. Ngati mawu aliwonse opanda phindu atuluka m'lilime lanu, pangani kukhala chizolowezi kunfunira zabwino Mtumiki (Salat-'Alan-Nabi) kamodzi kapena katatu nthawi yomweyo.

Chinsinsi cha m'nzake wa Mtumiki chokhala m'modzi mwa anthu aku paradizo

Ndi chisomo cha Allah عَزَّوَجَلَّ, Mneneri wathu wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ amatha kuzindikira mwa kuyang'ana anthu chabe kaya ngati adzapita ku Paradizo kapena kumoto, ndipo kwenikweni iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ amadziwa asanafike mlendo watsopano ngati adzapita ku Paradizo kapena ku Jahannama. Pa nkhanayi, tsiku lina Mneneri wa Rahmah, Nkhala pakati wa Ummah, Mwini Jannah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, 'Munthu woyamba amene adzalowe pakhomo lino akupita ku paradizo.' Pambuyo pake, Sayyiduna 'Abdullah Bin Salam رَضِيَ اللهُ عَنْهُ analowa. Anthu anamuyamikira ndipo anafunsa za ntchito imene anachita

yomwe inamupangitsa kuti apeze dalitso limenelo. Sayyiduna ‘Abdullah Bin Salam رَضِيَ اللهُ عَنْهُ anati, ‘Ntchito zanga zabwino ndi zochepa kwambiri, ndipo zimene ndili nazo chiyembekezo kwa Allah عَزَّوَجَلَّ ndi kuteteza ntima ndi kusiya kulankhula zopanda phindu.’ (As-Samt ma’ Mawsu’ah Ibn Abid Dunya, vol. 7, tsamba. 86, Hadees 111)

Mawu akuti الصَّدْرَ سَلَامَةً mu Hadees yodalitsidwayi, kutanthawuza ‘Kuteteza ntima’ amanthawuza kuyera kwa ntima kuchokera ku maganizo oyipa ndi matenda a n’kati monga nsanje ndi zina zotero, komanso kukhalapo kwa Iman (chikhulupiro) cholimba chokhazikika muntima.

Raftaar ka guftaar ka kirdar ka day day

Har ‘uzoo ka day mujh ko Khuda Qufi-e-Madinah

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 66)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Zitsanzo za mayankhulidwe opanda phindu

Okonedwa abale a Chisilamu! Ngakhale kulankhula zopanda phindu si tchimo, mulibe ubwino uliwonse mwa iwo. سُبْحَانَ اللهِ عَزَّوَجَلَّ Sayyiduna ‘Abdullah Bin Salam رَضِيَ اللهُ عَنْهُ anadalitsidwa ndi uthenga wabwino wa Paradise kuchokera m’lilime lodalitsika la Mneneri Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ! Khumbo limodzi limene iye رَضِيَ اللهُ عَنْهُ anali nalo ndilakuti sankadzilowetsa m’kulankhula

zopanda phindu. Iye رَحِيمِ اللَّهِ عَلَيْهِ sankafunsa mafunso pa nkhani zimene sizikumukhudza, koma mwatsoka ife timafunsa mafunso opanda phindu pa nkhani zimene tilibe nazo chidwi ngakhale pang'ono. Mwachitsanzo:

- ❖ Mwagula bwanji chimenechi?
- ❖ Mwapeza bwanji chimenecho?
- ❖ Kodi ntengo wa malo m'dera lakuti-lakuti uli bwanji?
- ❖ Ngati mukucheza m'nyumba ya wina kapena ngati wina wapeza nyumba yatsopano ndiye kuti mafunso amakhala akuti: Mwagula bwanji? Ili ndi zipinda zingati? lendi ndi bwanji? Kodi landilodi wanu ndi wotani? (Funso limeneli nthawi zambiri limayitanitsa miseche ndi kunena zabodza chifukwa nthawi zambiri yankho la funso limeneli popanda chifukwa cha Shar'i limakhala m'njira yochimwa: 'Landilodi wathu ndi wovuta / siwabwino/ woyipa / mchizi/ wozelezeka / woyipa ntima/ wowumira ndi zina zotero.')
- ❖ chimodzimodzinso pamene wina wagula shopu yatsopano, galimoto kapena njinga yamoto ndiye kuti mafunso amafunsidwa za ntengo wake, kulimba kwake, kaya agula ndi cash, kapena pa instalments.
- ❖ Anthu ena opanda nzeru akakacheza ndi wodwala amene sangathe n'komwe kulankhula chifukwa cha matenda,

amamufunsa mafunso ngati kuti iwo ndi ma dotolo akuluakulu ndipo amamufunsa tsatanetsatane komanso kufunsa mafotokozedwe ozama a zinthu monga ma ripoti aX-ray, zotsatira za ku labotale ndipo ngati pakhala opareshoni ngakhale chiwerengero cha zotsoka chimafunsidwa. Ngakhale kuli matenda okhudza ziwalo zachinsinsi, anthu opanda manyaziwa amafunsa tsatanetsatane poyera popanda kukayikira kulikonse. Akazi amapezekanso akuchita makambirano opanda nzeru ofanana ndi amenewa.

- ❖ Ndemanga zopanda phindu zimaperekedwa pa nyengo, makambirano osafunikira okhudza kukula kwa nyengo amayankhulidwa pafupipafupi popanda kusowa kulikonse mwachitsanzo m'nyengo yotentha anthu ena okonda kulankhula amakhala akunena kuti, 'Nyengo ikulentha kwambiri masiku ano ndipo tsoka! Kudulidwa kwa magetsi kulinso pafupipafupi.'
- ❖ Mofananamo, m'nyengo yozizira amapezeka akutentha mano chifukwa chotengera ena ndikunena kuti 'nyengo ya lero ikuzizira kowopsa.'
- ❖ Ngati kuli mitambo ndiye kuti ndemanga zosafunikira zimaperekedwa mwachitsanzo masiku ano kulinvula yopitirira muyezo, madzi adzaza paliponse ndipo akulu akulu okhudzidwa sakusamala kuchotsa matope ndi zina zotero.

- ❖ Mofananamo kudzudzula kopanda phindu pa ndale za m'dera lathu komanso zapadziko lonse kumachitika popanda cholinga chabwino chobweretsa kusintha ndipo mofananamo kudzudzula kosafunidwa pa zipani zandale zosiyanasiyana kumaperekedwa.
- ❖ Ngati wina wayendera nzinda wina kapena dziko lina, amayamba kufotokoza malo a mapiri ndi madyerero amene anawawona kumeneko kapena kufotokoza kwa nyumba ndi minsewu kumaperekedwa mosafunikira. Koma kumbukirani kuti ngati tinapeza wina akulankhula pamitu yotereyi tisamamuganizire zoyipa chifukwa nthawi zina kulankhula za nkhani za dziko ndi zolinga zabwino kumakhala ntchito ya Sawab kapena sikutera m'gulu la kulankhula zopanda phindu.

N'kovuta kwa amene amayankhula zopanda phindu kudziletsa ku tchimo la kukuza nkhani (kunama)

Kumbukirani kuti kulankhula zopanda phindu si tchimo, malingana ngati ndi zowona ndipo popanda kukokomezeka kapena kuchepetsa nkhani. Ngati kukokomezeka kulikonse kwachitika, kugwera n'gulu la kuchimwa. Koma ndikovuta kwambiri kufotokoza zinthu m'njira yoti isapitirire malire a 'kulankhula kosafunikira.'

Nthawi zambiri kukokomezeka kwabodza kumachitika, ndipo amene amayankhula zopanda phindu nthawi zambiri

amagwera m'dzenje la miseche, kunenera zaboroda, kupeza zolakwa mwa ena, komanso kupweteka maganizo a ena. Choncho, chitetezo kwenikweni chili m'kukhala chete, chifukwa 'Kukhala chete ndi golide.'

Bwenzi titalandira n'dalitso lodikira komanso kuyeza zomwe tilankhule

Ngati wina atakhala ndi chizolowezi cha 'kuyeza' kutanthawuza kusinkhasinkha mosamala asanalankhule, ndiye kuti ayamba kuzindikira mawu opanda phindu osawerengeka. Ngati ndi 'kulankhula zosafunikira' ngakhale kuti ili si tchimo, komabe pali zovuta zambiri mwa ichi, mwachitsanzo kupweteketsa lilime komanso kuwononga nthawi yantengo wapatali. Ngati nthawi yomweyo itagwiritsidwa ntchito pochita Zikr (kukumbukira) za Allah **عَزَّوَجَلَّ** kapena m'maphunziro a chipembedzo, kapena kufotokoza Sunnah ina, mphotho zochuluka zikhoza kupezeka.

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Zokambirana zopanda phindu zokhudza uchigawenga

Chimodzimodzi ngati pachitika chinachake cha uchigawenga **مَعَادَ اللهِ** anthu amapeza mutu wolankhulira zopanda phindu, ndipo nthawi zina amakhala ndi makambirano ochimwa. Amawutchula paliponse ndi mamasulidwe opanda mutu

kapena chiyambi kapena kulowa m'mikangano yopanda nzeru nthawi zina kunenera zabodza chipani china kapena mtsogoleri popanda umboni ndi zina zotero.

Nthawi zambiri zokambirana zoterezi sizikhala zopanda phindu chabe, m'malo mwake zimafalikira mantha komanso uchigawenga mwa anthu, zimalimbikitsa mphekesera, komanso zimakhala chifukwa cha chipiringu. Nafs umapeza chisangalalo chachikulu poyankhula ndi kunvetsera nkhani za kuphulika kwa mabomba komanso uchigawenga. Nthawi zina mawu opempha mapemphero amatchulidwa, koma chilakolako chopeza chisangalalo ndi kunva misisimuko kudzera poyankhula ndi kunvetsera nkhani zowopsa chimakhala muntima.

Ngati tingathe kuzindikira chinyengo cha Nafs chimenechi ndikupewa kukhala ndi chidwi pa kutchulidwa kwa kuphirika kwa mabomba komanso uchigawenga. Komabe, kutchula iwo amene aphedwa chifukwa cha kuponderezedwa, kusonyeza chisoni kwa Asilamu amene avulala kapena kukhudzidwa, kulankhula za momwe angathandizidwire, komanso kupanga mapembedzo (ma du'a) kuti pakhale bata ndi chitetezo siziyenera kuyimitsidwa, chifukwa ntchito zoterezi zimalipidwa. Choncho nthawi iliyonse pamene mukukumana ndi ntundu wotere wa makambirano, sinkhasinkhani mosamala kuti cholinga chanu ndi chani. Ngati mwapeza cholinga chabwino, ndiye kuti palibe vuto. Koma nthawi

zambiri cholinga cha zokambiranaz oterezi ndikupeza msisimuko pazochitika zowopsa.

Siddeeq-e-Akbar ankayika mwala n'kamwa mwake

Kumbukirani! Lilime nalonso ndi mphatso yayikulu ya Allah عَزَّوَجَلَّ ndipo lidzafunsidwa pa Tsiku la Chiweruzo, choncho lisagwiritsidwe ntchito molakwika. Sayyiduna Siddeeq-e-Akbar رَضِيَ اللهُ عَنْهُ, ngakhale anali Jannati (wolowa m'paradizo), anali wotsamala kwambiri ndi kuyipa kwa kagwiritsidwe tchito kwa lilime. Pa nkhaniyi, zatchulidwa mu Ihya-ul-'Uloom kuti, 'Sayyiduna Abu Bakr Siddeeq رَضِيَ اللهُ عَنْهُ anakonda kusunga mwala n'kamwa mwake pofuna kutsekereza mwayi wolankhula. (*Ihya-ul-'Uloom, vol. 3, tsamba. 137*)

Rakh laytay thay patthar sun Abu Bakr dahan mayn

Ay bhai! Zaban per tu laga Qufi-e-Madinah

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 66)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Kuphunzira kukhala chete kwa zaka 40

Okondedwa abale anga achisilamu! Ngati mukufunadi kukulitsa chizolowezi chokonda kukhala chete, ndiye kuti muyenera kuganizira mozama za nkhaniyi ndipo muyenera kuphunzira mwamphanvu, apo ayi ndikofunika kwambiri

kugwiritsa ntchito Qufl-e-Madinah palilime kudzera muzoyesayesa zapakatikati chabe. Kudziwopseza nokha ndi zowopsa zakugwiritsa ntchito lilime molakwika, pangani khama lalikulu kukulitsa chizolowezi chokhala chete; **إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ** kupambana kudzakhala kumapazi anu. Komabe, khama limeneli liyenera kupitirizidwa mwamphanvu. Tiyeni tiwone nkhani ya munthu amene anachita khama lotere. Sayyiduna Artaah Bin Munzir **رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ** wanena kuti, 'Munthu wina anayesesa kukhala chete kwa zaka 40 poyika mwala nkamwa mwake, mpaka kufika poti kupatula nthawi yakudya, kumwa, ndi kugona, sankachotsa mwala nkamwa mwake.' (*As-Samt ma' Mawsu'ah Ibn Abid-Dunya, vol. 7, tsamba. 256, Hadees 438*)

Kumbukirani! Mwala usakhale wawung'ono kwambiri kuti ungate kudutsa pakhosi ndikupangitsa ngozi, komanso mwala usasungidwe nkamwa muli munkhalidwe wa kusala chifukwa dothi ndi zina zotero kuchokera pamenepo zikhoza kudutsa pakhosi.

Woyera wa Taabi'i amene ankasinkhasinkha zokambirana zake polemba

Sayyiduna Rabi' Bin Khusaym **عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْكَرِيمِ** sanalankhule chinthu chilichonse cha dziko lapansi ndi lilime lake kwa zaka 20. Kumayambiriro kwa m'mawa, ankatenga cholemba, inki, ndi mapepala ndipo ankalemba chilichonse chimene angalankhule tsiku lonse kenako n'kudziwerengera madzulo

(malingana ndi zimene zinalembedwa). (*Ihya-ul-'Uloom, vol. 3, tsamba. 137*)

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Njira yodziwerengera pa zokambirana

Pano, mwa 'kudzifufuza', kumatanthawuza kulingalira mozama za mawu aliwonse amene ananenedwa ndi kudzifunsa mafunso, mwachitsanzo, dzifunsemi kuti, 'N'chifukwa chani ndinanena zakuti-nzakuti?' 'Kodi panali chifukwa chotani cholankhulira pa nthawi imeneyo?' 'Zokambirana zotere zikanatha kuchitika m'mawu ochuluka motere; n'chifukwa chani mawu owonjezera ananenedwa?' 'Mawu amene munanena kwa uyu ndi uyu anali osaloledwa ndi Shari'ah, ndipo anali chipongwe chimene chidzamupweteka m'mawu ake – tiyeni tilapeni tsopano ndiponso pemphani chikhululuko kwa m'bale wa chisilamu ameneyo.' 'N'chifukwa chani munapita ku nsonkhano umenewo pamene mumadziwa kuti zokambirana zopanda pake zidzachitika kumeneko, ndipo n'chifukwa chani munawonetsa n'gwirizano wanu pa chinthu chakuti-nchakuti? Munafunikira ngakhale kunvetsera miseche kumeneko, ndipo kwenikweni, munasangalalanso kunvetsera misecheyo. Tiyeni, tilapeni kuchokera pansu pa ntima, ndiponso dziperekeni kuti mudzakhale kutali ndi misonkhano yotere.' Mwanjira imeneyi, munthu wanzeru akhoza kudzifufuza pa zokambirana zake, ndipo kwenikweni pa

nkhani zake za tsiku ndi tsiku. Kudzera mwa izi, machimo anu, kusasamala, zofowoka zanu zambiri ndi zolakwa zanu zikhoza kudziwika kwa inu ndipo mutha kusankha kudzikonza. M'chikhalidwe cha Madani cha Dawat-e-Islami, kudzifufuza kumatchedwa 'Fikr-e-Madinah', ndipo Dawat-e-Islami imakhazikitsa malingaliro ochita Fikr-e-Madinah kwa mphindi zosachepera 12 tsiku lililonse komanso kulemba nkabuku ka Madani In'amaat.

Zikr-o-Durood her ghari wird-e-zaban rahay

Mayri fuuzool go`ee ki 'aanat nikaal do

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 164)

Umar Bin 'Abdul 'Azeez analira kwambiri

Sayyiduna Abu 'Abdullah رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ wanena kuti, 'Ndanva kuti katswiri wina anayamba kunena pamaso pa Sayyiduna 'Umar Bin 'Abdul 'Azeez رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ kuti, 'Katswiri wachete alinso ngati katswiri amene amalankhula.' Iye anati, 'Ndikuzindikira kuti pa Tsiku la Chiweruzo katswiri amene amalankhula adzakhala wapamwamba kuposa katswiri amene amakhala chete, chifukwa amene amalankhula adzakhala atapindulitsa anthu, pamene amakhala chete adzakhala atadzipindulitsa yekha basi.' Katswiri ameneyo kenako anati, 'Ya Ameer-ul-Mu'mineen! Kodi simukudziwa masawutso a kulankhula?' Atanva zimenezi, Sayyiduna 'Umar Bin 'Abdul 'Azeez رَضِيَ اللَّهُ عَنْهُ anayamba kulira kwambiri.'

(As-Samt ma' Mawsu'ah Ibn Abid Dunya, vol. 7, tsamba. 345, Hadees 648)

Mulungu عَزَّوَجَلَّ amuchitire chifundo ndi kutikhululukira popanda chiwerengero chifukwa cha iye!

اٰمِيْنُ بِجَاہِ خَاتِمِ النَّبِيِّنَّ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ

Kufotokozero kwa nkhaniyi

Okonedwa abale anga achisilamu! Zinali zodabwitsa bwanji kusamala komanso kukhala ndi mantha ndi Mulungu عَزَّوَجَلَّ kwa makolo athu olungama. Komabe, palibe kukayika kuti kulankhula nkhani zachipembedzo komanso akatswiri osamala a chipembedzo, kupereka nkhani zolimbikitsa Sunnah ndi Muballighin ndi kuyitanira ku zabwino ndi zochita zonse zomwe sizili ndi kufanana ubwino wake kuposa kukhala chete. Komabe, mawu a katswiri ameneyo pa maso pa Sayyiduna ‘Umar Bin ‘Abdul ‘Azeez رَضِيَ اللهُ عَنْهُ akuti, ‘Kodi simukudziwa masawutso a kulankhula?’ analinso oyenerera ndipo anali ndi chiganizo chimenechi cha katswiri wodzipereka chimene pozindikira kuya kwake Ameer-ul-Mu`mineen anayamba kulira kwambiri chifukwa chowopa Mulungu عَزَّوَجَلَّ. Ngakhale kulalikira zabwino kuli kopindulitsa kwa anthu, pali chiwopsezo cha zowawa zingapo kwa wokamba nkhani mwiniyo. Mwachitsanzo, ngati wina ali mlaliki wabwino, ndiye kuti akhoza kugwidwa ndi masawutso osiyanasiyana chifukwa cha matamando ndi kuyamikiridwa kumene amalandira kuchokera kwa ena chifukwa cha luso lake lotha kulankhula monveka bwino, komanso luso lakulankhula, kapena chifukwa

chodziyesa kukhala ndi luso, kapena chifukwa chodziwona kukhala woyenera ndipo ena kukhala opanda pake, kapena pogwiritsa ntchito mawu ambiri anvekere ndi ziganizo zochititsa chidwi kuti asangalatse ena chifukwa cha zilakolako zapadziko lapansi komanso kudzilemekeza. Ngati ali ndi luso lolankhula Chiarabu, akhoza kulowa m'masawutso ogwiritsa ntchito ziganizo zachiarabu pafupipafupi muzokambirana ndi kulankhula kwake pofuna kusangalatsa ena. Momwemonso, aliyense amene ali ndi mawu abwino akhoza kuvutika ndi kunyada chifukwa cha matamando a onvera, kuwona mawu ake abwino ngati luso lake m'malo mowawona ngati dalitso lochokera kwa Mulungu **عَزَّوَجَلَّ**. Choncho chenjezo la Katswiri wa Umulungu ameneyo pa nkhani ya 'kulankhula' n'loyenera. Kwa mlaliki yemwe ali ndi makhalidwe oyipa ofanana ndi omwe atchulidwa pamwambapa, kulalikirira kungakhale sawutso lalikulu ndipo kungawononge moyo wake wapambuyo pake, ngakhale onvera atapindula ndi mawu ake.

Mankhwala apadera oyeretsera zokambirana kuchokera ku zopanda pake

Kwa iwo omwe akufunadi kuchepetsa zokambirana zawo, mankhwala apadera ochokera mu Ihya-ul-'Uloom akuperekedwa pano kuti asefe mawu awo, ndikuyetsa zokambirana zawo kuchokera ku mawu osayenera kapena osafunikira komanso zolakwa zina zosiyanasiyana. Malingana ndi kachidutswa ka mawu awulemu a Hujjat-ul-Islam,

Sayyiduna Imam Muhammad Bin Muhammad Bin Muhammad Ghazali عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْوَالِي: 'pali mitundu inayi ya zokambirana:

1. Zokambirana zovulaza kotheratu
2. Zokambirana zopindulitsa kotheratu,
3. Zokambirana zomwe zili zovulaza komanso zopindulitsa
4. Zokambirana zomwe mulibe vuto komanso phindu lililonse. Nthawi zonse ndikofunikira kupewa ntundu woyamba wa zokambirana zomwe zili zovulaza kotheratu, ndipo m'njira yomweyo m'pofunika kupewa ntundu wachitatu wa zokambirana zomwe muli phindu ndi vuto zonse. Ntundu wachinayi ukuphatikizidwa muzokambirana zopanda pake, chifukwa palibe vuto lililonse m'menemo komanso phindu lililonse, choncho kuwononga nthawi muzokambirana zotere ndi ntundu wa vuto nawonso. Tsopano kukhala ntundu wachiwiri wokha wa zokambirana mwachitsanzo, magawo atatu mwa anayi (75%) a zokambirana sali oyenera kugwiritsidwa ntchito ndipo kagawo kamodzi kokha mwa magawo anayi (25%) a zokambirana, komwe kuli kopindulitsa, kokerako ndiko koyenera kugwiritsidwa ntchito. Komabe, muzokambirana izi zomwe zili zoyenera kugwiritsidwa ntchito, pali chiwopsezo cha kudziwonetsera kosadziwika, kupanga nkhani, miseche, kukokomezeka konyenga, kuzunzika

polankhula za luso la munthu kapena kukhulupirika kwake ndi zina zotero. Kuwonjezera apo, ngozi zakugwera muzokambirana zopanda pake panthawi yokhala ndi zokambirana zopindulitsa, ndipo kenako kudzera mu izi kupita patsogolo komwe kumatsogolera ku machimo omwe akuchitidwa amagwirizananso ndipo kulowa kumeneku kuli kochenjera kwambiri kotero kuti sikutha kudziwika. Choncho ngakhale pa nthawi ya zokambirana zomwe zili zoyenera kugwiritsidwa ntchito, munthu amakhala ali pachiwopsezo. (*Ihya-ul-'Uloom, vol. 3, tsamba. 138*)

Munthu wopusa amalankhula asanaganize

Okonedwa abale anga achisilamu! Munthu wanzeru choyamba amayeza mawu ake kenako n'kuwatchula, koma munthu wopusa amalankhula mwadzidzidzi chilichonse chimene chili mu ntima mwake, ngakhale kuti zotsatira zake zimamubweretsera manyazi. Pa nkhaniyi, Sayyiduna Hasan Basri عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْقَوِي wanena kuti, 'Zinali zodziwika pakati pa anthu kuti lilime la munthu wanzeru limatsatira ntima wake, chifukwa amayang'ana kuntima kwake asanalankhule (mwachitsanzo, amaganizira mosamala ngati anene kapena ayi). Ngati kuli kopindulitsa amalankhula, apo ayi amakhala chete. Mosiyana ndi zimenezi, lilime la munthu wopusa limatsogolera ntima wake, popeza samavutikira kulingalira mwachitsanzo, chilichonse chimene chabwera palilime, amangochitulutsa.'

(*zachotsedwa mu: Tanbih-ul-Ghafilien, tsamba. 115*)

Njira yoyezera musanalankhule

Okondedwa abale achisilamu! Kumbukirani kuti Mtumiki wathu Wokondedwa komanso Wodalitsika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ sanalankhulepo mawu aliwonse opanda pake kuchokera palilime lake lodalitsika lachowonadi ndipo sanasekepo mokweza. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ akanakhala kuti ma Sunnah awa wokhala chete komanso kusaseka mokweza akanakhala wofala. kukanakhala kuti timakulitsa chizolowezi choyeza mawu athu tisanayambe kulankhula. Njira yoyezera ndi yakuti musanatulutse mawu palilime lanu, dzifunseni: ‘Kodi cholinga chonenera izi ndi chani?’ ‘Kodi ndikuyitanira aliyense ku zabwino?’ ‘Kodi pali zabwino zilizonse kwa ine kapena wina aliyense m’zimene ndatsala pang’ono kulankhulazi?’ ‘Kodi zimene ndatsala pang’ono kunenazi zili ndi kukokomeza kulikonse kumene kungandichititse tchimo lonena bodza?’

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

Potchula chitsanzo cha kukokomeza konyenga, Sadr-ush-Shari’ah, Badr-ut-Tareeqah, Mufti Muhammad Amjad ‘Ali A’zami عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللهِ الْقَوِي wanena kuti, ‘Ngati wina anabwera kamodzi ndipo akunena kuti anabwera kawiri, ndiye kuti ndi wabodza.’ (*Bahar-e-Shari’at, vol. 3, tsamba. 519*)

Komanso lingalirani motere: ‘Kodi ndatsala pang’ono kutamanda wina monyenga?’ ‘Kodi ndatsala pang’ono kunenera wina miseche?’ ‘Kodi maganizo awina aliyense

adzapwetekedwa chifukwa cha ine kunena zimenezi?' 'Ndikatha kulankhula kodi ndidzafunika kubweza mawu anga kapena kupempha chikhululuko chifukwa chodzinvera chisoni?' 'Kodi ndidzafunika kubweza mawu aliwonse amene ndalankhula chifukwa cha kutengeka maganizo?' 'Kodi ndidzawulula chinsinsi changa kapena cha wina?' Mutatha kuyeza musanalankhule ngakhale zitawoneka kuti zimene mudzanene zilizosapindulitsa kapena kovulaza, ndipo sili mphoto kapena tchimo, ngakhale zili choncho palinso vuto linalake pakulankhula chifukwa m'malo movutitsa lilime ndi kutchula mawu opanda pake ndi achabechabe, ngati munthu anena ﴿لَا إِلَهَ إِلَّا اللَّهُ مُحَمَّدٌ رَّسُولُ اللَّهِ﴾ kapena kunfunira zabwino Mtumiki (Salat-'Alan-Nabi) adzalandiradi mphoto yayikulu ndipo uku ndiko kugwiritsa ntchito bwino nthawi yantengo wapatali; kusalandira mphoto imeneyi mosakayikira ndi kuluza.

Zikr-o-Durood her ghari wird-e-zaban rahay

Mayri fuzool go`ee ki 'aanat nikaal do

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 164)

Njira yosonyeza kukhala chete

Okondedwa abale achisilamu! Ngakhale kuti kulankhula kopanda pake si tchimo, pali kuluza ndi zovuta zazikulu zomwe zimagwirizanitsidwa nazo. Choncho, m'pofunika kwambiri kupewa kulankhula koteroko. Kunakhala kuti!

tikugwiritsa ntchito ubwino wokhala chete pogwiritsa ntchito Qufl-e-Madinah palilime. Nkhani: Sayyiduna Muwarriq 'Ijli رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ akuti, 'Pali khalidwe limodzi lotere limene ndakhala ndikuyesetsa kulipeza kwa zaka 20 ndipo sindinapambane kulipeza mpaka panobe; komabe sindinasiye kufunafuna kwanga.' Iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anafunsidwa kuti, 'Kodi chinthu chofunika chimenecho ndi chani?' Iye رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ anayankha kuti, 'Kukhala chete.' (Az-Zuhd lil-Imam Ahmad, tsamba. 310, Hadees 1762) Aliyense wofuna kukhala chete azilankhulana pang'ono kudzera polemba kapena kudzera m'zizindikiro m'malo molankhula pogwiritsa ntchito lilime. Mwanjira imeneyi, chizolowezi chokhala chete chidzayamba kukula, إِنَّ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ. pa nkhaniyi, funso limodzi M'madani In'amaat mu malangizo okhala olungama operekedwa ndi Dawat-e-Islami mwachitsanzo: Kodi mwagwiritsa ntchito 'Qufl-e-Madinah ya lilime' kukulitsa chizolowezi chopewa kulankhula kopanda pake lero polankhulana m'njira ina kudzera m'zizindikiro, ndipo kosachepera kanayi polemba? Pa nthawi ya zoyesayesa zanu poyesa kukhala chete, n'zotheka kwambiri kuti mukhale opambana popewa zokambirana zopanda pake kwa masiku angapo, koma kenako chizolowezi cholankhula chikhoza kubwerera mmbuyo mmene chinalili kale. Ngakhale izi zitachitika, musataye ntima ndipo pitirizani kuyesa nthawi zonse. Ngati nzimu wanu uli wowona, ndiye kuti إِنَّ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ mudzapambanadi. Pa nthawi imene mukuyesesa kukhala chete, ndi bwino kumwetulira pankhope panu kuti pasakhale munthu amene angaganize kuti mwamukwiwira chifukwa cha

kukwinya nkhope pa nthawi ngati zimenezi pamene mukuyesera kukhala chete, nkwiyo wanu ukhoza kuwonjezereka, choncho, ngati wina alephera kunvetsa zizindikiro zanu, onetsetsani kuti simukutsanulira nkwiyo wanu pa iye, chifukwa izi zingachititse tchimo lopweteka maganizo ake. Kulankhulana kudzera m'zizindikiro. Mlendo kapena munthu amene sakukudziwani akhoza kukhumudwa polankhulana naye kudzera m'zizindikiro; choncho, muyenera kulankhula nawo pakafunika kutero. Kwenikweni, kulankhula kumakhala Wajib (kokakamiza) pazolankhula zingapo. Mwachitsanzo, poyankha Salam ya munthu amene mwakumana naye ndi zina zotero. Mukakumana ndi munthu, m'malo mogwitsa tchito zizindikiro ndi Sunnah kupereka Salam ndi lilime. Momwemonso, ngati wina agogoda pakhomo, ndipo m'modzi wa m'nyumbamo afunsa kuti ndani, amene ali panjayo asanene kuti, 'Madinah! Chonde tsegulani!', kapena 'Ndi ine', m'malo mwake ndi Sunnah kutchula dzina lake pa nthawi yoteroyo.

Itanani mwawulemu ndipo pezani mphoto

Kuyitana wina kapena kukopa chidwi cha wina polankhula kuti 'Shish shish' sizinveka bwino. Ngati mukudziwa dzina la munthuyo, musamuyitane ngakhale polankhula kuti, 'Madinah'; m'malo mwake muyitaneni ndi dzina lake kapena Kunyah (dzina lodyera) chifukwa kutero ndi Sunnah. Kwenikweni ndikofunika kwambiri kupewa kuyitana mawu opatulika akuti 'Madinah' m'zimbudzi kapena m'malo ena

oyipa. Ngati simukudziwa dzina, ndiye kuti malingana ndi miyambo imene ilipo pamalopo, muyenera kumuyitana m'njira yawulemu. Mwachitsanzo m'dera lathu, munthu wachinyamata nthawi zambiri amatchedwa, 'm'chimwene!' ndipo munthu wankulu nthawi zambiri amatchedwa, 'malume!' Mulimonsemo, nthawi zonse mukayitana wina, pangani cholinga cholandira mphoto yosangalatsa ntima wa wokhulupirira wowona, ndipo gwiritsani ntchito njira yosangalatsa kwambiri limodzi ndi kugwiritsa ntchito dzina la munthuyo, ndipo kuwonjezera apo, malingana ndi mmene zinthu ziliri, onjezerani mawu akuti 'm'chimwene' kumapeto, kapena ngati wachita Hajj, ndiye kuti 'Haji' akhoza kuyikidwanso kutsogolo. Amene wayitanidwayo anene kuti 'Labbayk' (kutanthawuza kuti, 'Ndilipo'). **اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ عَزَّوَجَلَّ!** Mchikhalidwe cha Madani cha Dawat-e-Islami, wina akayitanidwa, yankho lakuti 'Labbayk' nthawi zambiri limaperekedwa, lomwe limanveka bwino m'makutu, ndipo chimwemwe chikhoza kulowa mu ntima mwa Msilamu akanva izi. Kuwonjezera apo, nfuno yakuti maswahaba olemekezeka **رَضِيَ اللهُ عَنْهُمْ** ankayankha ku kuyitana kwa Mtumiki Wokondedwa komanso Wodalitsika **صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ** polankhula mawu akuti 'Labbayk!' atchulidwa mu Ahadees. Kuwonjezera pa izi, palinso umboni wa izi kuchokera m'moyo wachitsanzo wa Wali (woyera) wa Mulungu **عَزَّوَجَلَّ**. Pa nkhaniyi, pamene aliyense angapemphe chidwi cha mtsogoleri wankulu wa mamiliyoni a-Hanbalis, Sayyiduna Imam Ahmad Bin Hanbal **رَحِمَهُ اللهُ عَلَيْهِ** pofuna kumufunsa za chigamulo chinachake, iye

رَحْمَةُ اللَّهِ عَلَيْهِ nthawi zambiri ankayankha polankhula kuti 'Labbayk.' (*Manaqib Imam Ahmad Bin Hanbal lil-Jawzi, tsamba. 298*) Zatchulidwa m'buku lodziwika bwino la Masnoon Du'as Hisn-e-Haseen: Wina akakuyitanani, nenani 'Labbayk' poyankha.

(*Hisn-e-Haseen, tsamba. 104*)

صَلَّى اللَّهُ عَلَى مُحَمَّدٍ صَلَّى اللَّهُ عَلَى الْحَبِيبِ

ZODABWITSA ZITATU ZA MADANI ZOMWE ZINAWONEKERA CHIFUKWA CHA KUKHALA CHETE

1. Kuwona Mtumiki woyera chifukwa cha ubwino wa kukhala chete

Ichi ndi chidule cha kalata ya mlongo wina wa chisilamu: nditanvetsera nkhani yolimbikitsa Sunnah yokhudza ubwino wa kukhala chete kudzera pa kaseti imene inatulutsidwa ndi nthambi yofalitsa mabuku a Dawat-e-Islami, Maktaba-tul-Madinah, ndinayamba kuyesesa Qufl-e-Madinah mwachitsanzo, ndinayamba kukulitsa chizolowezi chokhala chete. Pasanathe masiku atatu ndinazindikira kuchuluka kwa mawu opanda pake amene ndinali kulankhula.

عَزَّوَجَلَّ! اَلْحَمْدُ لِلَّهِ Chifukwa cha Madalitso a kukhala chete, ndinayamba kuwona maloto abwino. Pa tsiku lachitatu la

zoyesayesa zanga zopewa zokambirana zopanda pake, ndinanvetsera nkhani ina yolimbikitsa Sunnah yotulutsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, yotchedwa 'Ita'at kisay kehtay hayn?' ('Kodi Kunvera Kowona N'chani?').

Usiku umene ndinapita kukagona, **اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ عَزَّوَجَلَّ** ndinalota nkhani imene inasimbidwa mu kaseti ija. Anali malo a nkondo ina, kumene Mtumiki Woyera **صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ** anatuma Sayyiduna Huzayfah **رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ** kukanenera za adani. Pamene Sayyiduna Huzayfah **رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ** anafika m'matenti awosakhulupirira, anawona mtsogoleri wa osakhulupirira Abu Sufyan (amene anali asanalowe Chisilamu) atayimirira pamenepo. Popeza mwayi umenewo, Sayyiduna Huzayfah **رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ** anakoka muvi pa uta wake, pamene mwadzidzidzi anakumbukira lamulo la Mtumiki Wokonedwa **صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ** (chidule chake chinali chakuti, 'Usayambitse chiphokoso'). Choncho, ponvera Ameer (m'tsogoleri) wake, Iye **رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ** analeka kuponya muvi uja. Kenako iye **رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُ** anapereka zimene anapeza pa maso pa Mtumiki Wokonedwa komanso Wodalitsika **صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ**.

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ عَزَّوَجَلَّ! Ndinadalitsidwa ndi kuwona Mtumiki Wankulu ndi Wopatulika koposa **صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ** komanso maswahaba awiri olemekeseka **رَضِيَ اللّٰهُ عَنْهُمَا** monveka bwino; malo ena onse ankawoneka osadziwika bwino.

Linalembedwa patsogolo kuti: **اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ عَزَّوَجَلَّ** Chifukwa cha khama la masiku atatu okha lopewa zokambirana zopanda

pake, Mtumiki wa Rahmah, nkhala pakai wa Ummah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anandipatsa chaphindu chodabwitsa chotere. Tsopano ndikufuna kwambiri kuletsa lilime langa kutulutsa mawu aliwonse opanda pake. Chonde ndipemphereni kuti ndipambane m'khama langa.

Alongo achisilamu makamaka akhoza kuchitira nsanje mlongo mwayi umenewu. Kwa mlongo wachisilamu, kukhala chete ndi ntchito yovuta ndithu, chifukwa poyerekeza ndi amuna, akazi nthawi zambiri amayankhula kwambiri.

Allah zaban ka ho 'ata Qufi-e-Madinah

Mayn kash zaban per loon laga Qufi-e-Madinah

(wasail-e-bakhshish, tsamba. 66)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

2. Udindo wa kukhala chete pokhazikitsa chikhalidwe cha Madani

Ichi ndi chidule cha kalata imene m'bale wachisilamu anatomiza kwa Sag-e-Madinah (mlembi): Ngakhale kuti ndinali wokondwa ndi dera la Madani, ndinali wolankhula kwambiri ndipo sindinkawerenga Salat-'Alan-Nabi mu chiwerengero choyenera ndisananvetsetse nkhani yolimbikitsa Sunnah yokhudza kukhala chete mu Sunnah-Inspired Ijtima' ya Dawat-e-Islami.

Kuyambira pamene ndinayamba kulimbana ndi kukhala chete, ndakhala ndi mwayi wobwerezabwereza Salat-'Alan-Nabi kambirimbiri tsiku lililonse. Komanso, chifukwa cha khalidwe langa lolankhula kwambiri, ntchito ya Madani ya Dawat-e-Islami m'dera langa la Zayli Halqah inali yovuta. Masiku angapo apitawo, nsonkhano wa Madani Mashwarah unachitika pofuna kuthetsa kusanvana kwa m'dera lathu la Zayli Halqah. Chodabwitsa n'chakuti, chifukwa cha kukhala chete kwanga, **اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ عَزَّوَجَلَّ** mikangano yonse inatha.

Nigran-e-park wathu anawonetsa kusangalala kwake ndipo anandiwuza mowona ntima kuti, 'ndinali ndi mantha kwambiri kuti mwina mungayambe kutsutsana ndipo zokambirana zingasanduke mikangano kapena ndewu, komabe chifukwa cha kukhala chete kwanu, tonse tinanva kukhala pantendere.'

Kunena m'mbuyomu, chilengedwe cha misonkhano yathu ya Madani mashwarah chinkasokonekera chifukwa cha kutsutsana kwanga kopanda nako maziko komanso khalidwe langa lawukali

صَلُّوا عَلَيَّ الْحَبِيبِ صَلَّى اللهُ عَلَيَّ مُحَمَّدٍ

Chida cha Madani pa ntchito za Madani

Okonzeka abale achisilamu! Kodi mwawona momwe kulili kopindulitsa pa ntchito ya Madani kupewa nkhani zopanda

phindu! Choncho, mlaliki wa Sunnah ayenera kukhala wozama komanso ayenera kulankhula pang'ono. Ngati ali wolankhulitsa kwambiri kapena kumadula mawu ena akamalankhula, kapena kumalankhula mobwerezabwereza pamene ena akulankhula, kapena kuyambitsa mikangano ndi kusemphana maganizo, ndiye kuti pali chiwopsezo chachikulu chowononga nkhani zachipembedzo chifukwa cha iye. Munthu watsoka wotereyu amamanidwa mwayi wokhala chete, chomwe ndi chinthu china cha Madani chogonjetsa Satana. Popereka uphungu kwa Sayyiduna Abu Zar Ghifari رَضِيَ اللهُ عَنْهُ, Mtumiki wa Rahmah, nkhalapakati wa Ummah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, '(Iwe) uyenera kukhala chete kwambiri, chifukwa Satana athawa ndi zimenezi ndipo udzapeza mwayi m'zochitika zachipembedzo.'

(Shu'ab-ul-Iman, vol. 4, tsamba. 242, Hadees 4942)

Allah is say pehlay Iman pay maut day day

Nuqsan mayray sabab say ho Sunnat-e-Nabi ka

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 108)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

3. Udindo wa kukhala chete pokhazikitsa chikhalidwe cha Madani m'nyumba

Okondedwa abale achisilamu! Mwakusiya chizolowezi

cholankhula zosafunikira, kuseka ndi kuselewura, komanso kugwiritsa ntchito mawu amwano, ulemu wanu udzakulanso m'nyumba mwanu. Ngati anthu a m'banja mwanu achita chidwi ndi khalidwe lanu lozama, ndiye kuti kuyitanira kwanu ku zabwino kudzakhala ndi mphanvu mwachangu, ndipo ngati Madani Mahaul sanakhazikitsidwe m'nyumba mwanu, kudzakhala kosavuta kukhazikitsa.

Pa nkhaniyi, chidule cha kalata yomwe m'bale wina wachisilamu analemba atanva ulaliki wolimbikitsa wa Sunnah wokhudza 'Ubwino wokhala chete' mu mu sonkhano wa Ijtima' wa Dawat-e-Islami, uli motere: Malingana ndi ziphunzitso zomwe zinaperekedwa mu ulaliki wa Sunnah, munthu wolankhulitsa ngati ine anayamba kukhala ndi chizolowezi chokhala chete. Ndikupeza phindu lalikulu kwambiri chifukwa cha zimenezi. Chifukwa cha khalidwe langa lolankhula zopanda phindu, anthu a m'banja langa anali osakhutira nane, koma kuyambira pamene ndinayamba kukhala chete, mbiri yanga panyumba yakula kwambiri.

Makamaka, mayi anga okonededwa, omwe anali osasangalala nane, tsopano ali okondwa kwambiri ndi ine. M'mbuyomu, popeza ndinkalankhula zopanda phindu, ngakhale mawu anga abwino analibe mphanvu, koma tsopano nthawi iliyonse yomwe ndimawawuza za Sunnah ndi zina zotero mayi anga okonededwa, samangonvera ndi chidwi chokha, komanso amayesetsa kuchita zimenezo.

Berhta hay khamoshi say waqar ay mayray piyaray

Ay bhai! Zaban per tu laga Qufl-e-Madinah

(Wasail-e-Bakhshish, tsamba. 66)

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Ngale 19 za Madani zokhazikitsa chikhalidwe cha

Madani m'nyumba

1. Mukamalowa kapena kutuluka nyumba, nenani Salam mokweza.
2. Ngati mutawona bambo kapena amayi anu akubwera, imirirani kuti muwalemekeze.
3. Abale achisilamu ayenera kumpsompsona manja abambo awo komanso mapazi amayi awo, ndipo alongo achisilamu ayenera kumpsompsona amayi awo.
4. Chepetsani mawu anu pamaso pa makolo anu, musawayang'ane m'maso; gwetsani maso anu polankhula nawo.
5. Chitani mwamsanga ntchito iliyonse imene angakupatseni ngati siyosemphana ndi Shari'ah.
6. Khalani wozama panzeru. Pewani kulankhula mwawukali, kuseka ndi kusewera mopambanitsa, kukwiya pa tinthu

tating'ono, kupeza zolakwika pa chakudya, kudzudzula kapena kumenya azing'ono anu, kapena kukangana ndi akuluakulu a pakhomo. Ngati muli ndi chizolowezi chotsutsana, muyenera kusintha khalidwe lanu nthawi yomweyo ndikupempha chikhululukiro kwa aliyense.

7. Ngati mukhala wozama m'nyumba komanso kunjia kumene— **إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ** Madalitso a chinthu ichi adzalowa m'nyumba mwanu.
8. Lankhulani ndi amayi anu komanso amayi a ana anu (ngakhale ana omwe, kunjia kapena m'nyumba) mwa ulemu. (Pamene mukulankhula mu Urdu, itanani ena pogwiritsa ntchito 'Aap' m'malo mwa 'Tu').
9. Gona pasanathe maola awiri kuchokera nthawi ya 'Isha Jama'at ya pa m'nsikiti m'dera lanu. Ngati n'kotheke, dzukani pa Tahajjud kapena, dzukani mosavuta pa Fajr, ndipo pemphani Salat-ul-Fajr m'zere wakutsogolo mu msonkhano wa mu nsikiti. Mukachita izi, simudzanva ulesi kuntchito kwanu.
10. Ngati anthu a pakhomo ali ndi ulesi popemphera Salah, kapena ngati akuchita machimo osavala moyenera, kuwonera mafilimu ndi masewero a zisudzo, kapena kunvetsera nyimbo, ndipo inu sindinu nkulu wa pakhomopo, komanso mukukhulupirira kuti pali kuthekera kwakukulu kuti sanva uphungu wanu, m'malo

mowadzudzula nthawi zonse, alimbikitseni kunvetsera kapena kuwonera audio/video ma Bayanaat otulutsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, ndipo alimbikitseni kuwonera Madani Channel. **إِنْ شَاءَ اللَّهُ عَزَّوَجَلَّ** mudzawona zotsatira zolimbikitsa za Madani chifukwa cha zimenezi.

11. Chilichonse chomwe mungadzudzulidwe pakhomo, kapena ngati mungamenyedwe, pirirani, pirirani, ndipo pirirani. Ngati mungayambe kubwezera, ndiye kuti palibe mwayi wokhazikitsa chikhalidwe cha Madani m'nyumba mwanu, ndipo kunena zowona izi zitha kuyipitsa zinthu. Ngati nkhanza zosafunikira zikawonetsedwa, Satana nthawi zina amapambana popangitsa anthu kukhala amakani pobwezera.
12. Njira imodzi yabwino kwambiri yokhazikitsira chikhalidwe cha Madani pakhomo ndiyo kupereka kapena kunvetsera Dars kuchokera mu buku la Faizan-e-Sunnat pakhomo tsiku lililonse.
13. Pitirizani kuchita Du'a yochokera pansu pa ntima kwa aliynse wa pakhomo panu, monga momwe Mtumiki Wokondedwa **صَلَّى اللَّهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ** ananenera kuti: **الدُّعَاءُ سِلَاحُ الْمُؤْمِنِ** kutanthawuza kuti 'Du'a ndi chida cha okhulupirira owona.' (*Al-Mustadrak lil-Haakim, vol. 2, tsamba. 162, Hadees 1855*)
14. Pa nkhaniyi, pamene pakhomo patchulidwa, amayi omwe akukhala m'nyumba za apongozi awo azitenga kuti ndi

nyumba ya apongozi awo, ndipo pamene makolo patchulidwa, azichita ulemu womwewo kwa apongozi awo aakazi ndi aamuna, malinga ngati palibe chopinga cha Shar'i. Koma mkazi asapsompone manja kapena mapazi a apongozi ake aamuna, ndipo mwamunanso asachite chimodzimodzi kwa apongozi ake aakazi.

15. Zatchulidwa patsamba 290 la Masaail-ul-Quran: Werengani Du'a iyi pambuyo pa Salah iliyonse (ndi Salat-'Alan-Nabi kamodzi poyamba komanso kamodzi pambuyo pake) – **اِنَّ شَاءَ اللّٰهُ عَزَّوَجَلَّ** a pakhomo panu adzatsatira Sunnah zodala ndipo chikhalidwe cha Madani chidzakhazikika pakhomo panu. Du'a ili motere

[اَللّٰهُمَّ] رَبَّنَا هَبْ لَنَا مِنْ اَزْوَاجِنَا وَذُرِّيَّتِنَا قُرَّةَ اَعْيُنٍ

وَاَجْعَلْنَا لِلْمُتَّقِيْنَ اِمَامًا¹

(**اَللّٰهُمَّ** si gawo la vesi la Quran).

16. Kwa mwana wosanvera, kapena aliyense wa pakhomo wotere, akagona, werengani vesi ili lodala la Quran tsiku

¹ O our Lord, grant us from our wives and children the coolness of eyes, and make us leader of the pious ones.

[Kanz-ul-Iman (Translation of Quran)] (Part 19, Surah Al-Furqan, verse 74)

lililonse kwa masiku 11 kapena 21 m'mbali mwa bedi lake chakumutu ndi mawu oti asadzuke:

بِسْمِ اللَّهِ الرَّحْمَنِ الرَّحِيمِ ط

بَلْ هُوَ قُرْآنٌ مَّجِيدٌ ﴿٢١﴾ فِي لَوْحٍ مَّحْفُوظٍ ﴿٢٢﴾¹

kuyamba Ndi Salat-‘Alan-Nabi kamodzi komanso kamodzi pamapeto pake). Kumbukirani! Pochita ndi munthu wankulu wosanvera, pali mwayi woti adzuke ngati Wazifah iyi itawerengedwa mokweza, makamaka ngati ali tulo topepuka. N'zovuta kudziwa ngati wina wangotseka maso kapena wagona ndithu. Choncho, pamene pali chiwopsezo cha nkangano, musachite mwambo umenewu. Makamaka nkazi asachitire mwamuna wake mwambo umenewu.

17. Kuwonjezera apo, kuti ana osanvera akhale onvera, werengani ﴿يَا شَهِيدُ﴾ kakhumi ndi kamodzi (21) tsiku lililonse pambuyo pa Salat-ul-Fajr mukuyang'ana kuthambo, mpaka cholinga chanu chikwaniritsidwe. (Ndi Salat-‘Alan-Nabi kamodzi poyamba komanso kamodzi pambuyo pake).

¹ Rather it (what they deny) is the Excellent Glorious Quran, in the Preserved Tablet.

[Kanz-ul-Iman (Translation of Quran)] (Part 30, Surah Al-Burooj, verse 21, 22)

18. Khalani masiku anu amoyo molingana ndi Madani In'amaat. Komanso, limbikitsani anthu a m'banja lanu omwe ali ndi mitima yofewa mwanzeru komanso mofatsa kuti agwiritse ntchito Madani In'amaat. Atate ayesetse kukhazikitsa Madani In'amaat mwa ana awo mwanzeru komanso mofatsa. Ndi chifundo cha Allah عَزَّوَجَلَّ, kusintha kwa Madani kudzabwera m'nyumba.
19. Yendani osachepera masiku atatu mwezi uliwonse ndi okonda Mtumiki mu Madani Qafilah ndipo mupempherenso banja lanu kumeneko. Chifukwa cha Madani Qafilah, miyambo yapadziko lonse ya nyumba zingapo yasinthidwa kukhala chikhalidwe cha Madani .

Okonedwa abale achisilamu! Tsopano chakumapeto kwa Bayan yanga, ndikufuna kugwiritsa ntchito mwayi uwu kukuwuzani za ubwino wa Sunnah ndipo pambuyo pake ndikuwuzani zina mwa Sunnah ndi makhalidwe abwino. Mtumiki Wokonedwa Muhammad صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَآلِهِ وَسَلَّمَ anati, 'Iye amene akonda Sunnah yanga, wandikonda ine, ndipo iye amene wandikonda ine adzakhala nane limodzi m'Paranaiso.'

(Ibn 'Asakir, tsamba. 343, vol. 9)

*Seenah tayri Sunnat ka Madinah banay Aqa
Jannat mayn parausi mujhay tum apna banana*

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Madani 20 okhudza Miswak

Choyamba, mawu awiri a Mtumiki Woyera ﷺ:

1. Rak'at ziwiri zopempheredwa pambuyo pogwiritsa ntchito Miswak ndi zabwino kuposa Rak'at 70 zopemphedwa popanda Miswak. (*Attargheeb Wattarheeb, vol. 1, tsamba. 102, Hadees 18*)
2. Pangani kagwiritsidwe ntchito ka Miswak kukhala kofunikira pa inu nokha chifukwa mwa ichi muli ukhondo wa nkamwa komanso chifukwa chopezera chidwi (chopeza) chisangalalo cha Allah ﷻ. (*Musnad Imam Ahmad, vol. 2, tsamba. 438, Hadees 5869*)
3. Patsamba 288 la buku loyamba la Bahar-e-Shari'at, lofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yofalitsa mabuku a Dawat-e-Islami, 'Allamah Maulana Mufti Muhammad Amjad 'Ali A'zami ﷺ wanena kuti, 'Akatswiri olemekeseka akunena kuti aliyense amene amagwiritsa ntchito Miswak nthawi zonse, adzadalitsidwa ndi mwayi wowerenga Kalimah (maziko a chikhulupiro) pa nthawi ya infa, ndipo aliyense amene amadya chamba (zozunguza ubongo) sadzapatsidwa mwayi wowerenga Kalimah pa nthawi ya infa.'
4. Kwafotokozedwa kuchokera kwa Sayyiduna Ibn 'Abbas رضى الله عنهما kuti mwa Miswak muli mikhalidwe 10: Imayeretsa ikamwa, imalimbitsa nkhamu, imalimbitsa

maso, imachotsa chiseyeye (mamina a pachifuwa), imachotsa fungo loyipa la nkamwa, imagwirizana ndi Sunnah, angelo amasangalala, Allah عَزَّوَجَلَّ amakondwa, amawonjezera ntchito zabwino komanso imakonza m'mimba. (*Jam'-ul-Jawami' lis-Suyuti, tsamba. 249, vol. 5, Hadees 14867*)

5. Sayyiduna 'Abdul Wahhab Sha'rani سَيِّدُ التَّوَّابِيْنَ akufotokoza kuti, 'Pa nthawi ina Sayyiduna Abu Bakr Shibli Baghdadi عَلَيْهِ رَحْمَةُ اللَّهِ الْهَامِيْ anasowa Miswak pamene ankachita Wudu, ndipo anafunafuna koma sanathe kuwupeza. Choncho anagula Miswak pa dinar imodzi (ndalama ya golide) ndikuwugwiritsa ntchito. Ena anamufunsa kuti, 'Mwawononga ndalama zambiri pa chinthu ichi! Kodi munthu ayenera kuwononga ndalama zambiri chonchi pa Miswak?' Iye anayankha kuti, 'Popanda kukayika, dziko lino pamodzi ndi zonse zomwe zilimo sizili ndi phindu ngakhale lofanana ndi phiko la udzudzu pa maso pa Allah عَزَّوَجَلَّ. Kodi ndidzatani poyankha ngati pa Tsiku la Chiweruzo, Allah عَزَّوَجَلَّ atandifunsa kuti, 'N'chifukwa chani unasiya Sunnah ya wokondedwa wanga? Chowona cha ndalama ndi chuma chomwe ndinakupatsa sichili ngakhale chofanana ndi phiko la udzudzu, nanga n'chifukwa chani sunawononge chuma chonyozeka chotere pokwaniritsa Sunnah yayikulu imeneyi (Miswak)?' (*zatengedwa kuchokera mu: Lawaqah-ul-Anwaar, tsamba. 38*)

6. Sayyiduna Imam Shaafi'i **قُدَيْسٌ سَيِّدُهُ الثُّورَانِي** wanena kuti, 'Zinthu zinayi zimalimbisa nzeru: Kupewa nkhani zopanda phindu, kugwiritsa ntchito Miswak, kukhala ndi anthu opembedza komanso kuchita zinthu molingana ndi chidziwitso (cha chipembedzo) chomwe uli nacho.' (*Hayatul-'Haywan, vol. 2, tsamba. 166*)
7. Miswak iyenera kukhala wa Zaytoon, kapena Neem, kapena mitengo/zomera zofanana ndi zimene zili ndi kukoma kowawa.
8. Kukhutala kwa Miswak kuyenera kukhala kofanana ndi chala chaching'ono.
9. Miswak usakhale wotalika kuposa utali wa chikhato cha dzanja limodzi chifukwa Satana amakhalapo.
10. Tizitsitsi ta Miswak tiyenera kukhala tofewa; apo ayi, titha kupanga mpata pakati pa mano ndi nkhamu.
11. Ngati Miswak uli watsopano ndiye kuti ndi wabwino kwambiri; apo ayi uviyike m'galasi la madzi mpaka ufewe.
12. Dulani tizitsitsi ta Miswak tsiku lililonse chifukwa timakhala topindulitsa pokhapokha ngati tili ndi kukoma kowawa.
13. Tsukani mano anu mopingasa ndi Miswak.
14. Nthawi zonse tsukani mano anu ndi Miswak katatu.

15. Ndipo muziwutsuka (Miswak) pambuyo pogwiritsa ntchito nthawi iliyonse.
16. Gwirani Miswak mu dzanja lamanja m'njira yoti chala chaching'ono chikhale pansi pake ndipo zala zitatu zapakati zikhale pamwamba pake pamene chala chachikulu chikhale m'mbali mwake chitalozera kuntunda (kufupi ndi tizitsitsi tofewa tomwe timagwiritsidwa ntchito kutsuka mano).
17. Choyamba tsukani (ndi Miswak) mano akumanja akuntunda, kenako akumanzere akuntunda. Kenako yeretsani mano akumanja apansi ndipo kenako akumanzere apansi.
18. Kugwiritsa ntchito Miswak mowugwira polumikiza nkhonya kumabweretsa chiwopsezo cha zotupa za m'mutu.
19. Miswak ndi Sunnah yotsogolera Wudu koma ngati munthu ali ndi fungo loyipa nkamwa, kugwiritsa ntchito Miswak kumakhala Sunnat-ul-Muakkanah. (*Fatawa Razawiyyah, vol. 1, tsamba. 623*)
20. Musataye Miswak wogwiritsidwa kale ntchito kapena tizitsitsi take chifukwa ndi china chomwe chimagwiritsidwa ntchito potsata Sunnah. M'malo mwake, muwusunge kwinakwake mwawulemu, muwuyike m'nthaka kapena muwuponye m'nyanja. (*Kuti mupeze nfundo*)

zozama pa nkhanayi, onani tsamba 294 mpaka 295 la buku loyamba la Bahar-e-Shari'at, lofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah)

Kuti muphunzire Sunnah zambiri, gulani mabuku awiri ofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah: (1) Bahar-e-Shari'at gawo-16, lomwe lili ndi masamba 312. (2) Sunnatayn aur Anab lomwe lili ndi masamba 120. Njira imodzi yabwino kwambiri yophunzirira Sunnah ndikuyenda ndi ma Madani Qafilah a Dawat-e-Islami olimbikitsa ma Sunnah.

*Lootnay rahmatayn Qafilay mayn chalo
Seekhnay Sunnatayn Qafilay mayn chalo*

*Haun gi hal mushkilayn Qafilay mayn chalo
Khatm haun shamatayn Qafilay mayn chalo*

*Kuti mulandire chifundo, yendani ndi Madani Qafilah
Kuti muphunzire Sunnah, yendani ndi Madani Qafilah*

*Kuti muchotse zovuta, yendani ndi Madani Qafilah
Kuti muthetse masawutso, yendani ndi Madani Qafilah*

صَلَّى اللهُ عَلَى مُحَمَّدٍ

صَلُّوا عَلَى الْحَبِيبِ

Perekani kabukuka kwa munthu wina mukamaliza kuwerenga

Pezani mphoto pogawa timabuku tofalitsidwa ndi *Maktabatul-Madinah* komanso timapepala tating'ono tili ndi makhalidwe a ngale za *Madani* pa nthawi ya ukwati, maliro, *Ijtima'aat*, 'Urs, msonkhano wa *Milad* ndi zina zotero. Pangani chizolowezi chosunga timabuku tina m'sitolo mwanu kuti muzipereka kwa makasitomala anu monga mphoto ndi cholinga chopeza mphoto. Tumizani osachepera kabuku kamodzi kolimbikitsa *Sunnah* kapena kapepala kali ndi ngale za *Madani* m'nyumba iliyonse ya m'dera lanu mothandizidwa ndi ana kapena anyamata ogawa manyuzipepala, powonjezera khama lofalitsa kuyitanira ku chilungamo ndikupeza mphoto yayikulu.

KOCHOKERA MAWUMBONI

Al-Firdaus bima Saur-ul-Khattab, Dar-ul-Kutub ‘Ilmiyyah, Beirut

Al-Munabbihat, Peshawar

Al-Mustadrak, Dar-ul-Ma’rifah, Beirut

Al-Mustatraf, Dar-ul-Fikr, Beirut

Al-Qaul-ul-Badi’, Muwassasa-tur-Riyan, Beirut

As-Samt ma’ Mawsu’ah, Al-Maktaba-tul-‘Asariyyah, Beirut

As-Sunan-ul-Kubra, Dar-ul-Kutub ‘Ilmiyyah, Beirut

Bahar-e-Shari’at, Maktaba-tul-Madinah, Karachi

Fatawa Razawiyah, Raza Foundation, Lahore

Hisn-e-Haseen, Al-Maktaba-tul-‘Asariyyah, Beirut

Ihya-ul-‘Uloom, Dar Saadir, Beirut

Ithaf-us-Sanah, Dar-ul-Kutub ‘Ilmiyyah, Beirut

Jam’-ul-Jawami’, Dar-ul-Kutub ‘Ilmiyyah, Beirut

Kashf-ul-Mahjoob, Nawa-e-Waqt Printers, Lahore

Lawaqah-ul-Anwaar, Dar Ihya-ut-Turas Al-‘Arabi, Beirut

Manaqib Ahmad Bin Hanbal, Dar Ibn Khuldoon, Beirut

Minhaj-ul-'Aabideen, Dar-ul-Kutub 'Ilmiyyah, Beirut

Mirat-ul-Manajih, Zia-ul-Quran Publications, Lahore

Mirqat-ul-Mafatih, Dar-ul-Fikr, Beirut

Musnad Imam Ahmad, Dar-ul-Fikr, Beirut

Sahih Bukhari, Dar-ul-Kutub 'Ilmiyyah, Beirut

Sharh-us-Sunnah, Dar-ul-Kutub 'Ilmiyyah, Beirut

Shu'ab-ul-Iman, Dar-ul-Kutub 'Ilmiyyah, Beirut

Sunan-ut-Tirmizi, Dar-ul-Fikr, Beirut

Tanbih-ul-Ghafilien, Dar-ul-Kitab-ul-'Arabi, Beirut

Tareekh Baghdad, Dar-ul-Kutub 'Ilmiyyah, Beirut

Tareekh Dimashq, Dar-ul-Fikr, Beirut

Wasail-e-Bakhshish, Maktaba-tul-Madinah, Karachi

Kufalikira kwa Sunnah

Mwa chisomo cha Allah, Sunnah za Mtumiki wokondedwa komanso wodalala **مَنْ رَدَّ رَأْيَهُ عَنِ الْإِسْلَامِ جَحِيمًا يُخْرَجُ مِنْهَا طَيِّبًا فَحَسْبُ لَهُ الْجَهَنَّمُ بِمَا كَفَرَ وَكَانَ ظَالِمًا لِنَفْسِهِ** zinafanziridwa ndi kuphuziridwa kwambiri m'chikhaliwe chabwino cha Madani cha Dawat-e-Islami, loowe ndi bungwe la driko lonse losatengako mbuli mu ndale lokhodzara ndi kufalitsa kwa Quran ndi Sunnah.

Ndi pempho la Madani kuti muzikhala usiku wonse pansoekhano wa sabata iliyonse wolimbikitsa Sunnah (Ijtima) wonwe umayamba pambuyo pa Swalaat-ul-Maghrib Lachinayi lililonse mu nzinda wanu. Drizolowezeni kuyenda pa nthawi yake mu Madani Qafilah pamodzi ndi anthu okonda Mtumiki Woyera pofuna kuphuzira Sunnah, komanso kulemba akabuku ka Madani In'amat tsiku lililonse pochita Fikr-e-Madinah (kulingalira kwa Madani) ndipo mupereke kwa Zimmarad (woyimira Dawat-e-Islami) wa n'dera lanu.

Kudnera mwa madalitso a zimenezi, madrakhala ndi malingaliro komanso chikhumbi choteteza chikhulupiriro chanu, kutsatira Sunnah, komanso kudana ndi machimo. Mbale alyense wa Chislamu ayenera kukhala ndi malingaliro a Madani akuti: "Ndiyenera kuyesetsa kudzikonza ndekha komanso anthu a driko lonse lapansi."

Pofuna kudzikonza tokha, tiyenera kutsatira Madani In'amat, ndipo pofuna kukonza anthu a driko lonse tiyenera kuyenda Madani Qafilah, In-Sha-Allah.



Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 7213

Web: www.dawateislami.net | E-mail: translation@dawateislami.net